


AHEBRI, MUTU

WACHISANU NDI CHIMODZI ³

 Mmawa wabwino, abwenzi. Ndi chamwayi kukhala tiri pano. N—ndipo kuti ukwaniritse malonje aakulu awa ochokera kwa abusa athu ndithudi zingatengere moyo weniweni, sichoncho izo? Kotero ife tikupereka matamando kwa Ambuye chifukwa cha mphamvu Zake zonse zazikulu za machiritso ndi zifundo Zake zomwe Iye wazipereka kwa ife kudutsa mu zaka zonsezi.

Tsopano ine ndiri ndi zolengeza zingapo zoti ndipange. Chimodzi, ife, M'bale Woods ndi M'bale Roberson, ndipo ife tikufuna kuti tikuthokozeni inu nonse chifukwa chotipempherera ife, kuti tikhale ndi ulendo wotetezeka. Tinali ndi nthawi yodabwitsa; tinangopita kwa masiku anai ndi theka, ine ndikukhulupirira, ndipo tabwereranso motetezeka. Ambuye anataliditsa ife.

⁵⁰⁶ Tsopano, ife tikulengeza kuti M'bale Graham Snelling, chitsitsimutso chake, chikupitirirabe, uko ku—kumapeto kwa Msewu wa Brigham, m. . . mu mzindawu kuno. Ndipo Lachitatu likubwerali usiku. . . Ine ndikufuna kuti ndichokepo mawa, ukadzatha mwambo wa maliro omwe ine nditi ndilengeze mu mphindi pang'ono. Ife tidzakudziwitsani inu Lachitatu usiku. Ife tikufuna tidzapite mwa nthumwi, tonse, uko kuti tikamuhezere M'bale Graham asanatseke msonkhano wake kumeneko. Ndipo ife tidzayesera kuwutengera mpingo wonse palimodzi, ngati ife tingathe, ndi kupitako ngati nthumwi kuti tikakomane, kukakhala naye M'bale Graham mu umodzi wa misonkhano yake.

⁵⁰⁷ Ndipo, tsopano, madzulo ano k—kwa gulu loyikitsa maliro ku Charlestown, ndi—Akazi a Colvin, omwe nthawiyina ankabwera ku tchalitchi kuno zaka zambiri zapitazo, a usinkhu wa zaka sevente foro, achoka mmoyo uno dzulo apita kuti akakhale ndi Ambuye Yesu. Ndipo maliro ake ali woti akalalikidwa Lolemba, ndi Abusa Bambo McKinny, anali, kale, m'busa wa mpingo wa Methodist k—ku Port Fulton kwa zaka zambiri, yemwe anali bwenzi laolao kwa iwo. Ndipo ine ndi woti ndikamuthandizire iye, Lolemba, ku, ine ndikukhulupirira kuti ikakhala hafu pasiti wani, k—ku kachisi ku Charlestown, Indiana. Ndipo nonse inu abwenzi a banja la a Colvin mungatero, ine ndikudziwa, angakayamikire tsopano chilimbikitso pang'ono basi kapena k. . . kuwagwira dzanja pang'ono. Pakuti ife tonse tikudziwa chomwe izo ziri, ife omwe

tadutsapo mu zimenezo, mu zigwazo, ifeeni, ndipo tikudziwa chomwe izo zimatanthauza kuti utaye mzako. Ndipo chotero ife. . . Iye ali m—mu kachisi tsopano, ku Chartlestown, Indiana. Ngati inu muti mupite uko madzulo ano, bwanji, izo zikanati zikayamikiridwe ndi banja la a Colvin, ine ndikutsimikiza. Ambiri a anthu awo amabwera kuno ku kachisi panobe. Ine ndawakwatitsapo, ndawaikapo mmanda, ndawabatizapo, pafupifupi ndithu, banja lawo, lonse. Ndipo chotero Bambo Grayson, yemwe anali woyandikana naye wathu komwe kuno, ndi woyikitsa maliro kumeneko.

508 Ndipo ndiye ichi, usikuuno, Ambuye akalola, pamene ife titi tilekezere mmawa uno, ife tidzayesera kuti tidzatengerepo usikuuno, mu kuphunzira kwakukulu uku komwe ife tikuphunzira tsopano. Ndiyeno ine ndikuganiza kuti izo zinali zolengeza, monga momwe—monga i—ine ndikuzidziwira. Ndipo Lachitatu likubwerali usiku, tsopano, ife tidzalengeza usiku lomwe ife titi tidzakakhale ndi M'bale Graham.

509 Ndipo ife tikuwalandira alendo onse mu zipata zathu. Ndipo ndife okondwa kukhala ndi inu pano mmawa uno, ndipo tikupemphera kuti Mulungu mopitirira, mochuluka, akudalitseni inu lero chifukwa cha kusonkhana uku.

510 M'bale Cox wangondiuza ine kuti zotulutsira mawuzi sizinali kugwira bwino ntchito pa kanthawi. Izo mwinamwake, kapena chifukwa cha nyengoyi, muli chinyezi chambiri, mu zotulutsira mawuzo apo. Ndipo izo si ziribwino mokwanira, pa kuyamba pomwe, chotero icho chikhoza kukhala chomwe chikupangitsa.

511 Pamene ine ndikumuwona mlongo wakhala apayu yemwe ine ndikumudziwa, Mlongo Arganbright. I. . . Izi si zabwino n—ndi zamakhalidwe, kuti ndifunse izi, koma kodi inu mwamvapo kuchokera kwa M'bale Arganbright kuchokera pamene iye anapita uko. Ine ndiri wokondweretsedwa kwambiri kuti ndimve kuchokera kwa iye mwamsanga pamene ife tingakhoze. Iye ali ku Switserland ndi Germany, mu msonkhano cha kumeneko ndi M'bale Tommy Hicks ndi Paul Cain. Ngati inu mungamve konse, Mlongo Ruth, inu mundidziwitse ine apo pomwe, mwamsanga basi monga inu mungakhozere.

512 Tsopano, kachisi wamng'onoyu alibe umembala, koma ife tiri ndi chiyanjano. Ife tiribe kachikhulupiriro koma Khristu, tiribe lamulo koma chikondi, tiribe bukhu koma Baibulo. Ndilo Bukhu lokha lomwe ife timalidziwa, ndi chinthu chokha chomwe ife timachidziwa, chomwe ife tiri nacho. Pamene Magazi a Yesu Khristu akutitsuka ife ku machimo onse, ife tiri nacho chiyanjano wina ndi mzake, aliynense.

513 Ine ndimazindikira, mmawa uno, kwa anthu ena inu mwina munamumva m'bale akupemphera. Amene uja anali wa Chikatolika, chomwecho, kapena kale anali wa Chikatolika.

Ndipo ife tiri ndi mitundu yonse ya anthu amabwera kuno. Ndinangokhala nawo mwayi, mphindi zingapo zapitazo, kuti ndigwirane chanza ndi m'bale wa Chimennonite yemwe wakhala muno. Ndipo kuchokera kwa a Chimennonite, kuchokera kwa a Chimethodisti, kuchokera kwa a Chibaptisti, ndi a Chikatolika, kapena aliyense yemwe angathe, aloleni iwo azibwera. Ndipo ife tizisonkhana palimodzi mozungulira pa madalitso a Mawu a Mulungu. Pomwe pano pali a Mboni za Yehova ndi anthu a mitundu yosiyana, ndawona azipembedzo zosiyana.

514 Ine kale ndinkakonda (chabwino, ine ndimatero panobe) Kumadzulo. Ine ndimakonda akavalo ndi ng'ombe. Ine ndinaleredwera ku farmu basi, ndipo i—ine ndimakukonda uko. Ndipo ife kale tinkakhala ndi kukusa, ndipo ine ndinkakhoza kupita nawo. Ndipo ife tinali ndi mpanda wa kulowerera. Ine sindikudziwa ngati inu anthu Akummawa mukudziwa chomwe mpanda wa kulowerera, uli kapena ayi. Ndi pamene inu muziika ng'ombe mu—nkhalango, izo zimayenera kukhala ndi mpanda woziteteza izo kuti zisamalowerere chomwe iwo amachitcha, bwerera mmbuyo kodyetsera komwe. Izo zikanamakhoza kukadya nsipu wonse, kumene iwo amaweta nsipu woti azidzazidyetsera nthawi ya chirimwe. Ndiyeno mpaka mmapi, iwo ankakhalanso ndi mipanda ya kulowerera, komwe iwo amalekanitsa zazikazi zochuluka chotero ndi zazimuna, ndi zina zotero. Iwo umatchedwa mpanda wa kulowerera. Koma mpanda waukulu wa kulowerera ndi pamene woyang'anira amaima pamene ng'ombe zikudutsa.

515 Ndipo tsopano ine ndinkakhala pamenepo, masiku ambiri, pa chishalo changa, ndi kumaziyang'ana izo pamene ng'ombe zinali zikudutsa. Apo pankakhala mitundu yonse yosiyana inkalowa mmenemo. Panali zina zimatchedwa “Diamond.” Ndipo zina za izo zinkatchedwa “Bar X.” Ndi zina... Zathu zinali “Tripod,” chinachake chonga chizindikiro cha a Boy Scout. Ina yotsatira, mmusi mwa izo, inali “turkey track” pa kavalo. Ndipo iwo anali ndi mitundu yonse yosiyana, k—kuti azizidziwa ng'ombe zawo pamene iwo akuzitulutsa izo ankazitsogolera izo kwina.

516 Tsopano, woyang'anira sanali ndi chidwi kwambiri ndi mtundu womwe izo zinali nazo, koma ichi ndi chomwe, woyang'anirayo anali nacho chidwi kuyang'ana kokolekedwa mu khutu la izo. Chirichonse chomwe chinkalowa mmenemo, ziribe kanthu kuti mtundu womwe izo zinali, izo zinkayenera kukhala ziri mtundu weniweni wa Hereford. Izo sizinkakhoza kulowa mmenemo kupatula ngati zinali za Hereford. Zinkayenera kukhala ziweto zolembetsedwa kapena izo sizikanakhoza kulowamo.

517 Ine ndikuganiza, pa tsiku ilo pamene Ambuye abwera, Iye sadzapereka chidwi chirichonse ku mtundu womwe ife tavalala, koma ngati ife tonse tiri Akhristu obadwa-kachiwiri.

Ndiko kulondola. Ndizo ziweto za Khristu. Kuyesa kwa Magazi kudzatitsimikizira ife, ife tonse tiri Akhristu. Ndipo ngati ife tonse titi tikakhale mwanjira imeneyo *kumeneko*, ife kulibwino mwina tikhale mwanjira imeneyo kuno. Kodi inu simukuganiza chomwecho? Ndiyo njira yake, ife tikuyamikira chiyanjano chonse kuchokera ku mipingo yonse yosiyana.

⁵¹⁸ Tsopano ife tikuphonzira mu Bukhu lodala ili la Ahebri. M'bale mmodzi walimva kukoma kwambiri ilo mpaka iye watenga matepi ndipo iye akupanga bukhu la zokaphunzitsa pa izi.

⁵¹⁹ Tsopano ife tikuti tifike, posachedwa apa, ku mutu wa 11. Ife tikuyembekeza kuti tidzatsiriza chirimwe pa umenewo, pa mutu wa 11. Pa lirilonse la makhalidwe amenewo, ife tikukhumba kuti tidzabwerere kudutsa mu Bukhuli ndi kudzamingiriza Lemba lonselo palimodzi. Ine ndimati ndidzachite izo. Ine ndimachita mwa kagawo, pa ina iyi, ya mitu yapitayi, kuti tidzalitenge Bukhu lonselo nkulimangiriza palimodzi. Pakuti, inu mukuona, Lemba liyenera kutsimikizira Lemba.

⁵²⁰ Chotero, ngati pali kutsutsana kulikonse, komwe wina aliynse akanaganiza kuti Malemba amatsutsana okha, uko ndi kulakwitsa. Palibe Lemba lomwe limatsutsa Lemba. K—kutsutsana kuli pamene mwinamwake Ilo limatsutsa njira yathu yomwe ife timayang'anira pa Ilo, koma Iwo samatsutsana Iwowokha. Ine ndakhala ndiri mu utumiki, ndikupitirira kwa zaka twente-sikisi tsopano, ndipo ine sindinayambe, nthawi imodzi, ndapezapo chinthu chimodzi mu Baibulo chimene chimatsutsana ndi china chirichonse chimene chinalembedwa mu Baibuloli. Ndipo i—ine ndikungodziwa kuti izo mulibe umo.

⁵²¹ Ndipo lero ife tikuphonzira mu umodzi wa mitu yodala ya Ahebri, mutu wa 7. Ndipo pakakhala aliynse yemwe alibe Baibulo, angafune kuti azititsatira ife mu kuwerenga, ife tingakhale okondwa kukubweretserani inu Baibulo ngati inu mungati mungokweza dzanja lanu. Ine ndikhala ndi akuluakulu ena, winawake, abwere kuno ndi kudzatenga ena. Ena akuimika manja awo kumbuyo uko. Ndipo zikomo inu, m'bale. Ndipo ngati inu mukufuna Baibulo, ingokwezani dzanja lanu, ndipo iwo alibweretsa ilo kwa inu.

⁵²² Tsopano, njira yokha yomwe mpingo ungakhoze kumangidwa, njira yokha yomwe munthu angapezere Chikhulupiriro, si mwa chipembedzo chake, si mwa oyanjana nawo ake. Koma Chikhulupiriro chake chimakhala osati pa fioroje ya malingaliro a munthu winawake, chifukwa ziri, mochuluka kapena mochepera, zonse palimodzi za munthu. Koma njira yokha yomwe Chikhulupiriro chingakhoze kupezera malo otsimikizika ake okhazikikirapo, ndi pa Mawu osasinthika ndi osasinthika a Mulungu. "Chikhulupiriro chimadza pa kumva, kumva Mawu." Ndi momwe izo

zimatengera. N—ndipo pamene Chikhulupiriro chimvedwa ndi kulandiridwa, izo zimakhala kwa nthawizonse zokhazikika. Palibe chinanso chomwe chingachisunthe icho, ziribe kanthu zomwe zingabwere kapena kupita. Palibe chomwe chingasithe konse Chikhulupiriro chimenecho. Taganizani za zimenezo. Inu muli ozikika, ndipo inu simungati musinthenso, kwa nthawi ndi Muyaya. Inu mwazikika kwanthawizonse, “Pakuti Mulungu, mwa nsembe imodzi, wawapanga kukhala angwiro kwanthawizonse iwo omwe ayeretsewa, kapena aitanidwa.”

⁵²³ Ndipo Chikhulupiriro chiri nawo malo aakulu chotero mwa Mkhristu, moyo wa wokhulupirira, mwakuti icho chikhoza kutenga kuima kwake pa mphepete pa manda amatope kapena pamwamba pa chitanda, pamene mwana wofunikira kapena wokoma mtima wadutsa kuchokera ku moyo uno kupita kutsidyako. Ndipo ndi kuyang’ana kolimba kwa maso a mphungu, chikhoza kuyang’ana kwa Iye yemwe anati, “Ine ndine chiwukitsiro ndi Moyo.” Ndipo iwo amaiwala zinthu zomwe ziri zammbuyo. Iwo amalimbikira kumka ku malo a kuitana kwa pamwamba.

⁵²⁴ Ndine wokondwa kwambiri kuti Mulungu wapereka zoterozo, ndipo wazipanga izo kukhala mphatso yaulere kwa onse. Ndi chomwe mipingo ili yoti izikhala ichi. *Mipingo* simatanthauza zipembezoo kapena mabungwe; iyo imatanthauza, “Magulu a anthu, a okhulupirira, omwe amasonkhana palimodzi pansi pa chiyanjano cha Mawu.”

⁵²⁵ Ndipo mu kuphunzitsa kopambana uku apa kwa Paulo Woyera, mwa maziko, mu mitu ya mmbuyomu, iye mosindika wakhala akuchita ndi Umulungu wapamwamba wa Ambuye Yesu ndi yemwe Iye anali. Khristu anali Mulungu, anapangidwa chomwecho kuti munthu akanakhoza kumumverera Iye ndi kumukhudza Iye, n—ndi kuyanjana ndi Iye. Khristu, Ambuye Yesu, anali thupi lomwe Mulungu ankakhalamo, “Mulungu anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Timoteo Woyamba 3:16, “Popanda kutsutsana chinsinsi cha umulungu ndi chachikulu, pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi.”

⁵²⁶ Yehova Wamkulu anabwera pansi ndipo anadzapangidwa kukhala chogwirika, pakudzakhala mu thupi la Mwana Wake Yemwe, akulengeza ndi kuliyanjanitsira dziko kwa Iyemwini. Mulungu sanali china . . . Khristu sanali china choperewera kwa Mulungu, n—ndipo Mulungu sanali china choperewera kwa Khristu. Awiriwo palimodzi anapanga Umulungu mu thupi, anapangidwa motsikirapo pang’ono kuposa Angelo, chotero kuti Iye akanakhoza kuzunzika. Angelo sangakhoze kuzunzika. Yesu anali kachisi momwe Mulungu anali kukhalamo.

⁵²⁷ Baibulo linanena, mu mutu wa 7 wa Machitidwe a Atumwi, kuti, “Makachisi, ndi nsembe zopyereza ndi zopereka zopyereza Inu simunazifune, koma thupi Inu mwandikonzera

Ine. Ngakhale ziri choncho Wammwamba kwambiriyu sakhala mu nyumba zomangidwa ndi manja, koma thupi Inu mwandikonzera Ine,” apo pakukhala mu kachisi kapena kukhala mu chiyanjano ndi munthu.

⁵²⁸ Mulungu akalola, mwamsanga pamene tithana ndi mutu uwu pano, kapena tikatsiriza ndi Bukhu ili, ife tikufuna tipite mmbuyo ndi kukalitenga Bukhu la Rute ndi kusonyeza mmenemo momwe Mulungu anakhalira wachibale kwa ife, kuti awayanjantitse otaika abwerere kwa Iyemwini pochita chiyanjano ndi kukhala mmodzi wa ife. Wowombolayo ayenera kuti akhale wapachibale, ndipo njira yokha yomwe Mulungu akanakhala wapachibale kwa ife, ndi kukhala mmodzi wa ife. Chotero, Iye sakanakhoza kukhala Mngelo ndi kukhala wapachibale kwa munthu.

⁵²⁹ Usiku wathawu pamene ine ndinali kuyankhula kwa mwana wosweka mtima, wochita nane, za mayi omwe angomwalira kumene, anati, “O M’bale Bill, ine ndikulingalira iye ali Mngelo usikuuno.”

⁵³⁰ Ine ndinati, “Ayi, Earl. Iye sadzakhala konse Mngelo. Iye ali mkazi, usikuuno, monga momwe Mulungu anamupangira iye, ndipo nthawizonse adzakhala ali, osati konse Mngelo.” Mulungu anapanga Angelo. Iye sanapange konse anthu kuti adzakhale Angelo. Iye anapanga Angelo *ndi* anthu. Chotero anthu sadzakhala konse Angelo, ndipo Angelo sadzakhala konse anthu. Mulungu anawapanga iwo mosiyana.

⁵³¹ Tsopano, ndipo mwa Khristu anadzakhala thupi kuti adzawombole kuchokera ku chachikulu icho kutsidyako komwe munthu anali atagwerako, ndipo chisavundi chija mwa tchimo chinali chitabwera pansu, Mulungu anabwera pansu ndipo anadzatenga mawonekedwe a mawumbidwe a munthu, ndipo anadzakhala wapachibale kwa ife, kuti Iye akhoze kunyamula machimo athu ndi imfa yathu.

⁵³² Ndipo mu kumodzi kwa kufotokoza komwe ife tinali kukupereka, mu maphunziro ammbuyowa; maziko pang’ono chabe chotero obwera mwatsopano akhoze kumvetsa. Mulungu, ali paulendo Wake waku Kalvare. Pamene mbola ya imfa inali pa Iye, ndipo inali kulira momuzungulira Iye, ndipo potsiriza iyo inamuluma Iye mpaka Iye anafa. Iye anafa mpaka dzuwa linasiya kuwala. Iye anafa mpaka mwezi ndi nyenyezi sizikanakhoza kupereka kuwala kwawo.

⁵³³ Kapena, momwe Iye anayenera kuchitira izo, kuti azike mbola ya imfa! Ngati Iye akanakhala ali munthu wachisavundi, ngati iye akanakhala ali mu fiofane, kapena akanakhala ali mu mzimu, imfa simakhala ndi ulamuliro pa zimenezo. Iye ankayenera kudzakhala thupi, kuti Iye akanakhoza kutenga mbola ya imfa. Koma pamene njuchi kapena kachilombo kamene kamaluma, kakaluma kamodzi mwakuya, iko sikadzaluma

konse kachiwiri. Iko kamasiya mbola yake mu mnofuwo. Ndipo ndi chimene Khristu ali- . . . kapena Mulungu anakhala. Khristu anakhala mu mnofu, kuti Iye adzakhoze kuzika mu mnofu Wake Womwe mbola ya imfa. Ndipo pamene imfa inadzisolola pochoka pa Iye pa mtanda, iyo inasiyapo mbola yake, iyo singakhoze kumuluma wokhulupirira panonso. Iyo ikhoza kupanga phokoso long'ung'uzza, iyo ikhoza kulira ndi kuwopsyeza, koma iyo singakhoze kuluma. Iyo ilibe mbola.

⁵³⁴ Paulo Woyera wamkulu, pa kumka ku imfa yake, anafuula ndipo anati, “O imfa, mbola yako ili kuti? Ndipo manda, chigonjetso chako chiri kuti? Koma kuthokoza kupite kwa Mulungu yemwe watipatsa kale ife chigonjetso kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu, pakuti zonse imfa ndi manda zataya mphamvu zake.”

⁵³⁵ Tsopano, ndiye, Lamlungu lapitali ife tinatenga, “Kusiya zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu,” mu mutu wa 6, ife tinawerenga izi, “tiyeni ife tipitirire mpaka ku ungwiro.” Ndipo ife tinapeza kuti anthu lero mu mipingo yambiri, limodzi ndi kachisi wa Branham ndi ina yosiyana, ife timaika zochuluka kwambiri pa kuphunzira za zoyambirira za Khristu: Iye anali Mwana wa Abrahamu, Iye anali mwana w—wa *akuti-n-akuti*, ndi mpaka mmbuyo, mibadwo. Koma Baibulo linati, “Tiyeni ife tiyike kumbali zinthu zimenezo, ndi kupitirira mpaka ku ungwiro.”

⁵³⁶ Choyamba inu muyenera kuti muzidziwa chiphunzitso, ndiyeno inu muyenera kuti muzidziwa zinthu zonse izi; kenako tiyeni tiziziyika izo pambali, Iye anati, za chiukitsiro cha akufa, kusanjikapo kwa manja, maubatizo, ndi zinthu zonse zakufa izo za Mulungu. Komabe, i—izo ziribe Moyo mwa izo. Koma mpingo lero ukungomapita ku zinthu zimenezo, “O, ife timakhulupirira mu Umulungu wa Khristu.” Inde. Zedi. “Ife timakhulupirira mu ubatizo wa madzi.” Inde. Zedi. “Kusanjikapo kwa manja.”

⁵³⁷ Paulo anati, “Ife tizichita zonse izi ngati Mulungu alola. Koma pamaso pa izo zonse, tiyeni tiziyike izo pambali tsopano, ndi kupitirira mpaka ku ungwiro.”

⁵³⁸ Tsopano, mpingo sungakhoze kukhalitsidwa wangwiro kudzera mu mabungwe. Iwo amapita motalikira ndi Mulungu, nthawi zonse, kapena motalikirana kwa wina ndi umzake. Ife timaika malire, ife timadzilekanitsa tokha, mowonekeratu posakhala nacho Chikhulupiriro. Koma ndiye pamene ife tisiya zoyambirira izo za chiphunzitso, ngati ife tisunthira mpaka ku ungwiro, ndiye zinthu zazing'ono izo sizimakhala zogwiritsidwa ntchito kwambiri.

⁵³⁹ Ife timapita mu chiyanjano, ndipo ife tikupeza kuti njira yokha yomwe ife tingakhoze kukhalitsidwa angwiro ndi kukhala mwa Khristu. Ndipo ife tikupezapo ndiye, mwa zophunzitsa za Baibulo, za momwe ife timalowera mwa Khristu;

osati mwa ubatizo wa madzi, osati pa kusanjikapo kwa manja, osati mwa kuphunzitsa. “Koma mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi ndipo timakhalitsidwa angwiro kupyolera mu kuzunzika Kwake.” Ndiye, ife timayang’ana mosiyana. Ife timaganiza mosiyana. Ife timachita mosiyana. Ife timakhala moyo mosiyana. Osati chifukwa ndi mwa ntchito kapena ndife a pa mpingo, koma chifukwa cha “chikondi chimene Mulungu wachiyika mu mitima yathu ndi Mzimu Woyera,” izo zimatipanga ife kukhala mbadwa limodzi nawo mu Ufumu wa Mulungu, ndiye palibe chipembedzo kapena malire mmenemo. Ndife tonse Thupi limodzi lalikululu.

⁵⁴⁰ Tsopano ndife okonzeka kuti tilowe pa phunziro la mmawawu, mu mphindi zochepa. Chinthu chimodzi choonjezera chimene ine ndikanafuna kuti ndifikepo apa, icho ndicho, kuti, Paulo akuyankhula mu Bukhu, la 7... kapena mutu wa 6, ife tikupeza apa kuti ife timapangidwa kukhala angwiro mwa Khristu. Ndiye mu ndime ya 13 ya mutu wa 6, maziko pang’ono chabe.

Pakuti pamene Mulungu anapanga lonjezo kwa Abrahamu, chifukwa Iye sakanakhoza kulumbira pa wina wokulirapo, iye analumbirira pa iyemwini,

Mulungu analumbirira pa Iyemwini, chifukwa Iye sakanakhoza kulumbira pa wina wokulirapo.

⁵⁴¹ Tsopano ife tikufuna kuti tibwerere mmbuyo. Tiyeni titenge pa Agalatiya mphindi zochepa zokha. Tembenezirani ku Bukhu la Agalatiya, ndi kupeza Agalatiya 3:16. Ndipo ife tiwerenga apa mphindi yokha, pa yemwe Iye anamulumbirirapo.

Tsopano kwa Abrahamu ndi mbewu yake lonjezo linapangidwa. Iye sanati, Ndi kwa mbewu, ngati zambiri; koma ngati imodzi, . . . kwa mbewu, yomwe ili Khristu.

⁵⁴² Tsopano ngati inu mungazindikire, powerenga izo mwatcheru tsopano, pamene inu mukuwerenga.

. . . kwa Abrahamu ndi mbewu yake (imodzi) anali malonjezo (ochuluka) atapangidwira.

⁵⁴³ “Abrahamu ndi Mbewu yake.” Tsopano, Mbewu ya Abrahamu inali imodzi, yemwe anali Khristu; mwa choimira chotsogolera, Isaki.

Koma Abrahamu anali ndi ana ambiri. Iye anali naye wina iye asanakhale naye Isaki, chomwe chinkasonyeza kuteleleka mwa kusakhulupirira kwa Sara yemwe ankafuna Hana kuti abale mwanayo, kuganiza kuti iye anali wokalamba kwambiri, ndipo Mulungu kuti alambalale ndi kupanga njira inayake kwa njira yomwe Iye analonjeza kuti achitire izo.

⁵⁴⁴ Koma Mulungu amasunga lonjezo Lake. Ziribe kanthu momwe zingawonekere kuti ziri zosalinalirika, Mulungu

amakhala wokakamidzira ku lonjezo Lake. Ndipo Sara anaganiza kuti mwina akanakhala ndi Hana...kapena Hagara, kani, mdzakazi wake, kuti abale mwana kudzera mwa Abrahamu, ndipo iye akanadzamutenga iye. Ndipo ameneyo anadzakhala Ishmaeli, yemwe anali munga mu mnofu, kuyambira pamenepo mpaka pano. Akadali munga mu mnofu, chifukwa kuchokera apo kunadza Aluya, ndipo iwo nthawizonse akhala ali mwanjira imeneyo.

⁵⁴⁵ Tsopano, nthawi iliyonse yomwe iwe sukhulupirira Mawu apoyera a Mulungu ndi kutenga njira inayake, uwo udzakhala munga mu mnofu wanu kuchokera pamenepo mpakana. Inu muzitenga basi zomwe Mulungu ananena. Ngati Iye ananena Izo, izo ndi basi zomwe Iye akutanthauza. O, lodala likhale Dzina Lake! Muzingotenga Mawu Ake.

⁵⁴⁶ Ziribe kanthu omwe angayese kumalambalala, kuti, “Chabwino, Iwo ndithudi sakutanthauza Zimenezo.” Iwo amatanthauza basi zomwe Iwo akunena, pamene Mulungu apanga lonjezo.

⁵⁴⁷ Tsopano ngati ife tingazindikire mwatcheru.

... Abrahamu ndi mbewu yake anali malonjezo. . .

China chinali Mbewu, imodzi, ndi chimzakecho chinali malonjezo. Pali zopasa lonjezo limodzi, ndi oposa munthu mmodzi omwe ali owerengeredwa mu Mbewu ya Abrahamu. Mukuona? Pali Mbewu imodzi, koma anthu ambiri a Mbewuyo. Mukuona? Iwo anali osati a Abrahamu yekha, kapena kwa Isaki yekha. Koma. . . Iwo anali a kwa Mbewu yonse ya Abrahamu. Malonjezo anapangidwa kwa mbewu ya wina aliyense payekha wa Mbewu imeneyo. Inu mukumvetsa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

⁵⁴⁸ “Chotero, ife, pokhala okufa mwa Khristu, molingana ndi Malemba, ife timatengapo Mbewu ya Abrahamu ndi olandira molingana ndi lonjezo.” Osati pa kujowina mpingo, kapena kupanga kwa zikhazikitso zakufa, k—kapena zina zotero. Koma pa kukhala obadwa mwa Mzimu wa Khristu, ife ndife Mbewu ya Abrahamu, ndi olandira limodzi ndi Iye mu Ufumu.

⁵⁴⁹ Ndiye ife tikupitirira, kuti tiwerenge, ndiye, mopitirira pang’ono tsopano, “Mulungu akupanga lumbiriro.” Tsopano ndime ya 17 ya mutu wa 6.

Momwe Mulungu, pololela mochuluka kwambiri. . .

... Mulungu, pololela mochuluka kwambiri kuti asonyeze kwa olandira lonjezo kusalephera kwa uphungu wake, anatsimikizira izo ndi lumbiriro:

⁵⁵⁰ O, tiyeni tingopuma tsopano maminiti pang’ono. “Mulungu kulolela mochuluka.” Osati kuti Iye ankasowa kutero, koma kuti achipange ichi chinthu chotsimikizika.

551 Tsopano, ife tapeza kale kuti Mulungu anakhala thupi, anadzakhala pakati pathu, momwe Iye anadziwonetsera Iyemwini kwa dziko. Pamene Iye anamupeza mkazi mu chigololo, anati, “Ine sindiri. Ine sindiri kukutsutsa iwe. Pita, usakachimwenso.” Pamene Iye anapeza wodwala, Iye anachita basi mwanjira yomwe Iye akanayenera kuti achitire, pakuti Iye anali Mulungu, ndipo I—Iye amachiza wodwala. Iye amaukitsa akufa. Iye amakhululukira machimo. Zinalibe kanthu momwe iwo analiri, ndi ochuluka bwanji, ndi momwe analiri atabwererera mmbuyo, Iye anawakhululukira iwo, mulimonse, ngati iwo anali ololera kuti abwere ndi kudzapempha.

552 Tsopano zindikirani. Ngati Mulungu anachitapo pa nthawi ina iliyonse pa chochitika chinachake, ndipo ngati chochitika chimenecho chiukaponso, Iye ayenera kuti achite nthawi yachiwiriyo momwe Iye anachitira nthawi yoyamba kapena Iye ndi wosalungama. Mukuona? Ziribe kanthu momwe iwe uliri woyipa mu tchimo, kutsika kwake komwe iwe ungakhale, Iye ayenera kuti achite kwa iwe momwe Iye anachitira kwa mkazi wakugwa uja, kapena Iye anachita molakwika pajapa. Khalidwe la Mulungu ndilo Umunthu Wake, ndipo chimene Iye ali mu khalidwe Lake chimafotokoza Umunthu Wake.

553 Ndipo ndi momwe inu muliri, mu khalidwe lanu la moyo, limafotokoza chomwe inu muli. Monga ife tinali nazo ndipo tinadutsamo, phunziro kapena awiri apitawo, anthu Achimethodisti amafuna kulengeza kuti, “Pamene iwe ufuula, iwe uli nawo Iwo.” Achipentekoste amati, “Pamene iwe unayankhula mu malirime, iwe unaulandira Iwo.” Ogwedezeka ankati, “Pamene iwe ugwedezeka, iwe waulandira Iwo,” Ogwedezeka aku Pennsylvania. Ndipo ife tikupeza kuti iwo onse akulakwitsa. Moyo wako umafotokoza Izo. Umunthu wako umafotokoza chomwe iwe uli. Munthu amadziwika ndi zintchito zake, ndi chirichonse chomwe moyo wako uli.

554 Inu munaimvapo nkhani yakale, “Moyo wako ukuyankhula mofuula kwambiri, ine sindikutha kumwa mawu ako.” Chotero chirichonse chomwe iwe uli, iwe uli. Moyo umene iwe ukuukhala ukusonyeza mtundu wa mzimu umene uli mwa iwe.

555 Ndiyeno inu mukhoza kumasanziira chinthu cholakwika. . . kapena kusanziira chinthu cholondola, mwina ine ndinene. Inu mukhoza kusanziira Mkhristu. Koma padzafika, pang’ono ndi pang’ono, idzafika nthawi pamene kupsyinjika kudzaikidwapo, ndiye izo zidzasonyeza chomwe inu muli. Chingwe chimakhala champhamvu pa malo ake ofooketsa.

556 Pamene Khristu Mwana wa Mulungu anaikidwa ku mayesero, zinasonyeza chomwe Iye anali. Zedi. Pamene iwe uyikidwa ku mayesero, izo zitsimikizira chomwe iwe uli. Moyo wako nthawizonse umanyezimiritsira chomwe chiri mkati mwa

iwe. Pang'ono ndi pang'ono, khalani otsimikiza kuti machimo anu asadzakupezeni inu. Ndi chomwe ife tikuyesera kuchinena.

⁵⁵⁷ Yesu anati, mu Yohane Woyera 5:24, “Iye amene amva,” osati iye amene agwedezeke, iye amene ayankhula. Iye amene. . . “Iye amene amva Mawu Anga, nakhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo; koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.”

⁵⁵⁸ Ndi chikhulupiriro chanu. Ndipo chikhulupiriro chanu, chovomerezedwa ndi milomo yanu, chimawonetsera kwa anthu omwe angathe kumwa, koma moyo wanu ndi wotseguka pamaso pa onse. Koteru, ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe inu mukuyesera kudzychititsa *ichi* ndi kupanga *ichi*, izo sizidzagwira konse ntchito. Izo ziyenera kutkhala ziri mwa inu. Apo ndi pachimake penipeni pa nkhani yonseyo. Chikhulupiriro chanu chanu mwa Khristu woukitsidwa, monga Mpulumutsi wanu; kuti Iye ali pa dzanja lamanja la Mulungu, akuchita mu malo anu mmawa uno, pamene inu mukuchita mu malo Ake pansi kuno monga mboni. Mboni imachita mmalo mwa winawake, kukuimira inu ngati mboni. Ndipo pamene moyo wanu ukunyezimiritsa kuno chomwe umboni wanu uli mwa Khristu, iwo ukunyezimiritsa kumeneko ndipo iwo ukunyezimiritsa kuno. Ndipo Iye ali mmwamba umo, monga momwe Iye aliri kwa inu, akunyezimiritsa limodzi uko ndi kuno. Chotero inu muli. . . Mwa chikhulupiriro chanu, inu muli opulumutsidwa, ndipo icho chokha. Chotero, zogirigisha, zotengeka, zomverera, chirichonse, chiribe malo nkomwe mwa Ichu. Tsopano, osati. . .

⁵⁵⁹ Tsopano, musati muziganiza molakwika, kuti ine sindimakhulupirira mu zotengeka izi. Ndithudi. Koma pa chomwe ife tiri tsopano, kuyesera kukhomerera kwa anthu awa a tsiku lino, si zotengeka. Mdierekezi wazitenga zinthu zimenezo ndipo wapita nawo kuthengo anthu, kuwasiya iwo azikhazikitsa kopita kwawo kwa Muyaya pa zotengeka. Kufuula, kuyankhula ndi malirime, kumapita ku tchalitchi Lamlungu lirilonse, kumachita ngati Mkristu, izo sizidzakhala ndi chochita chimodzi pa tsiku limenelo. “Kupatula munthuyo atabadwa kachiwiri.” Ndipo moyo wanu kumanyezimiritsa chomwe inu muli mkatimo, mukuona, osati zotengeka zanu.

⁵⁶⁰ Inu mukhoza kukhala ndi magazi mmanja mwanu, inu mukhoza kuyankhula ndi malirime, inu mukhoza kumachiza odwala, inu mukhoza kusuntha mapiri ndi chikhulupiriro chanu, ndipo inu simuli kanthu apobe. Akorinto Woyamba 13. Mukuona? Ichu chiyenera kukhala chiri chinachake chomwe chinachitika mwa Kubadwa komwe kumabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo Mulungu amabweretsa kubadwa Kwatsopano mkati mwa inu, ndi kukupatsani inu gawo la Iyemwini. Ndiye zinthu zimenezo ziridi. Inu ndinu cholengedwa chatsopano. “Ine ndimapereka kwa iwo Wamuyaya.”

⁵⁶¹ Ife tinadutsa mu mawu oti “Muyaya.” *Kwanthawizonse* ndi “danga la nthawi.” *Umuyaya* ndi kwanthawizonse, kwanthawi za nthawi, koma pali Umuyaya umodzi wokha. Ndipo ife tikupeza kuti iwe umalandira Moyo Wamuyaya, ndipo mawu ake mu Chigriki ndi Zoe, omwe amatanthauza “Moyo wa Mulungu.” Ndipo iwe umalandira gawo la Moyo wa Mulungu, umene umakupanga iwe kukhala mwana wauzimu wa Mulungu, ndipo ndiwe basi wosatha monga Mulungu ali wosatha. Iwe ulibe mathero, ulibe malo olekezera, chifukwa iwe unalibe malo oti uyambirepo. Chirichonse chomwe chiri ndi chiyambi chiri nawo mathero, ndipo icho chomwe chiribe chiyambi chiribe mathero.

⁵⁶² Momwe ife tikuwakondera Mawu ofunika awo! Momwe Mkhristu ayenera kukhala wokhazikika mu Chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera, ndi kuti asamangokankhidwira uku ndi uko, malo kupita ku malo, ndi kumajowina mipingo yosiyanasiyana. Mpingo uliwonse womwe inu mukufuna kuti mukhale wa iwo ziribwino bwino, bola ngati inu muli Mkhristu. Koma poyamba yikani chinthu choyambirira, chomwe chiri Kubadwa uko komwe kumakupangitsani inu kukhala wapachibale kwa Mulungu, monga Mulungu anadzakhala wapachibale kwa inu.

⁵⁶³ Iye anakhala wapachibale, kuti iye adzakhoze kukuutsani inu. Iye asanakuutseni inu, Iye ayenera kuti akupatseni inu Moyo Wamuyaya. Ndiye Mulungu ankayenera kuti akhale wapachibale, kuti atenge imfa, kuti akuwukitseni inu. Ndiye inu muyenera kukhala wapachibale kwa Iye, polinga kuti inu mupite mu chiwukitsiro. Inu mukuona chomwe izo ziri? Izo zangokhala kusinthanitsana. Mulungu anakhala inu, kuti inu mukhoze kukhala Mulungu. Mukuona? Mulungu anakhala gawo la inu, mnofu, kuti inu mukhoze mwa chisomo Chake kukhala gawo la Iye, ndizo zonse, kuti mukhale nawo Moyo Wamuyaya.

⁵⁶⁴ Chithunzi chokongola basi, ndipo, o, ife tikuzikonda izi.

Tsopano, *Mulungu, kulolera mochuluka kwambiri* . . .

⁵⁶⁵ Samasowa kutero, koma Iye anali kulolera kutero. Ndine wokondwa kwambiri nazo zimenezo, sichoncho inu, kuti Mulungu wathu akulolera? Penyani. Bwanji ngati Iye—bwanji ngati Iye akanati asakhale wopirira-motalika? Kodi chipatso cha Mzimu ndi chiani? Chikondi, chimwemwe, chikhulupiriro, mtendere, kupirira motalika. Ilo ndi gawo la Mulungu lomwe liri mwa inu. Ndipo mukhoza kunyamulizana, kunyamulizana zolemetsa za wina ndi mzake. Kukhululukirana wina ndi mzake, monga Mulungu chifukwa cha Khristu anakukhululukirani inu. Mzimu wa Mulungu mwa inu umakupangitsani inu mwanjira imeneyo. Ndiyeno pamene Mulungu anali kuno pa dziko lapansi ndipo anadzakhala inu, anadzakhala tchimo, kuti Iye potenga tchimo lanu, anakunyamulirani inu ilo ndipo

analipirira chilango chanu cha izo. Mulungu ndi wopirira-motalika, wotinyamulira akatundu athu.

566 Ndiyeno Iye ndi Mulungu wabwino. Ngati inu mukufuna kuti, zinthu zina mwanjira yanu, inu mukudziwa, Mulungu ndi wabwino mokwanira kuti achita izo. Iye amakonda k—kuti akupangitseni inu kukondwa. Iye amafuna kutero. Iye, Iye ndi chikondi, ndipo chikondi Chake chachikulu chimamukakamiza Iye ngakhale kuti azitsika pansu nthawizina, kuti akuloleni inu kukhala ndi zinthu zomwe inu mukuzifuna.

567 Tayang'anani pa Tomasi, chitachitika chiwukitsiro. Tomasi sankakhoza kukhulupirira. O, iye ali nawo ana ambiri lero. Koma Tomasi anati, "Ayi. Ayi. Ine ndiyenera kuti ndikakhale nawo umboni winawake. Ine ndikuyenera kuti ndiike manja anga mu mbali Yake, ndi mu Zake...zala zanga cha apa m'manja Ake, ine ndisanakhulupirire Izo. I, ine sindikusamala zomwe inu mukunena." Mukuona, iye anali atachoka yense mu dongosolo la Lemba, apo pomwe. Inu mumayenera kuti muzikhulupirira Izo. Chotero iye anati, "Ine ndiyenera kuti ndikhale nawo mtundu wina wa umboni, kuti nditsimikizire Izo."

568 Ndipo Yesu anawonekera, Iye ndi wabwino, "Bwera pano, Tomasi, ngati icho ndi chomwe iwe ukufuna, chabwino, ndi zimenezotu. Iwe ukhoza kukhala nazo izo."

569 Ndi momwe ife tiriri. Iye timati, "Ambuye, ine ndiyenera kuti ndiyankhule ndi malirime. I—ine ndiyenera kuti ndifuule. Ine ndiyenera . . ."

570 "O, pitirirani nazo, ine ndikulolani inu mukhale nazo izo." Iye ndi wabwino.

571 Chotero iye anakhudza manja ake mmbali Mwake, ndiye iye anati, "O, ndi Ambuye wanga ndi Mulungu wanga."

572 Iye anati, "Tsopano, Tomasi, iwe wakhulupirira pakuti waona. Koma kuchuluka kwake kwa omwe alibe umboni ndipo komabe akukhulupirira Izo!" Ndi zimenezotu. Ndi pamene ife tiyenera kuti tifiikepo. "Kuchuluka kwake kwa mphoto ya omwe sanawone kanthu komabe akuzikhulupirira Izo." Ndi kuchita kwa chikhulupiriro, kuti ife tazilandirira Izo.

573 Tsopano, ine ndikukhulupirira zizindikiro zimatsatira okhulupirira, koma tiyeni tiziyike zinthu zoyamba poyamba. Inu mukhoza kukhala ndi zizindikiro, opanda Ichi. Paulo anati inu mukanakhoza. Iye anati, "Ine ndikanakhoza kumayankhula ndi lirime monga a onse anthu ndi Angelo; sindiri kanthu. Ine ndikanakhoza kusuntha mapiri ndi chikhulupiriro changa; ine sindiri kanthu. Ine ndikanakhoza kumamvetsa Baibulo, mwanjira yakuti ine ndikanakhoza kumadziwa zinsinsi zonse za Mulungu; ine sindiri kanthu." Mukuona, izo ndi mphoto za Mzimu Woyera, popanda Mzimu Woyera.

574 Mzimu Woyera ndi Mulungu. Mulungu ndi chikondi, chimwenwe, mtendere, kupirira motalika, kuleza, chipiriro. Umenewo ndi Mzimu wa Mulungu. Ndi zomwe Mulungu akuziutsa mu masiku otsiriza, kudzera mu Mzimu umenewo.

575 Tsopano, “Kusalola . . .”

. . . *Mulungu*, kulolera mochuluka *kuti* asonyeze *kwa olandira a lonjezo* . . .

. . . *Mulungu*, kulolera mochuluka . . . *kuti* asonyeze . . . *olandira* . . .

Kodi olandira ndi ndani? “Ife, pokhala okufa mwa Khristu, timatengera pa ife Mbewu ya Abrahamu, ndipo ndife olandira.” O, kodi izo zikulowera mkati? Ife ndife olandira a Ufumu wa Mulungu, kupyolera mu lonjezo lolumbiridwa. Mulungu sankasowa kuti alumbire. Mawu Ake ndi angwiro. Koma Iye analumbira, aponso, pa Iyemwini, pakuti uko kunalibe wina wamkulupo.

576 Pamene ife tikupitiriza kuwerenga, mphindi yokha, mvetserani.

. . . *lonjezo la kusalephera kwa uphungu wake, anatsimikizira ilo mwa lumbiriro:*

577 “Kusalephereka,” wasasinthath. Mulungu sangakhoze kusintha. Iye ayenera kumakhalabe yemweyo. Ndipo ngati Mulungu anamuchiza munthu mmodzi wodwala, Iye sangakhoze konse kusintha lingaliro Lake. Mulungu anamukhululukira wochimwa mmodzi, wachiwerewere mmodzi, Iye sangakhoze konse kusintha lingaliro Lake. Kusalephereka, kusasinthath kwa Mawu a Mulungu. Mulungu ananena, mu malo amodzi, “Ine ndine Ambuye yemwe ndimachiza matenda anu onse.” Iye ayenera kukhala ndi Chimenecho, pakuti Iye ndi wopandamalire. Iye ankadziwa mapeto kuchokera ku chiyambi.

578 Tsopano, ine ndikhoza kunena, “Ine ndichitha *ichi*.” Ndipo Baibulo linati, ife tikuyenera kumati, “Ngati Ambuye alola.” Chifukwa, ndine wachivundi. Ine sindikudziwa. Nthawizina ine ndimachitha kubweza mawu anga, koma Mulungu sangakhoze kubweza Ake. Iye ndi Mulungu.

579 Ndipo Iye anangotifunsa ife chinthu chimodzi, “Ngati inu mutati mukhulupirire.” O, mai! “Ngati inu mungathe kukhulupirira, zinthu zonse ndi zotheka.” “Ngati inu mutati mukhulupirire,” ndizo zonse. “Inu, ngati inu mungathe,” ndi limenelo funsolo. Koma sikuti funsolo liri pa Mawu a Mulungu, chifukwa, kusalephera Kwake, Iye sangakhoze kusintha. Kudabwitsa kwakeko!

580 Tsopano mvetserani, pamene ife tikuwerenga mpaka pansu.

Kuti mwa zinthu ziwiri zosalephereka, mu zomwe ndi zosatheka kuti Mulungu aname, . . .

Zosatheka! Kusatheka ndi kusalephereka mwakuchitika ndi mawu ofanana; sangathe kusintha, sangathe kusuntha. Izo ziyenera kukhala mofanana kwanthawizonse. Sizingatheke kusinthidwa, kusalephereka ndi kusatheka.

Ndipo ziwiri, *mwa zinthu ziwiri zosalephereka, mu zomwe kunali kosatheka kuti Mulungu aname, . . .*

“Ife tiri nazo zinthu ziwiri?” Inde. Choyamba, Mawu Ake anati Iye akanadzazichita izo. Chachiwiri chinali lumbiro Lake lolumbiridwa pa izo, Iye akanadzazichita izo. O, mai!

⁵⁸¹ Ndi mtundu wanji wa womwe ife tikuyenera kukhala? Chifukwa chiani kuti ife tizikankhidwira uku ndi uko ndi kumathamangira uku ndi uko, ndi kumatenga zinthu za mdziko ndi kumachita monga kapangidwe kochepetsedwa ka Chikhristu cha 1957 ichi? Ife tikufuna kuti tikhale mtundu wa kachitidwe kachikale komwe kamamutenga Mulungu pa Mawu Ake, ndi kumazitcha zinthu izo zomwe palibe, ngati kuti izo ziripo. “Ngati Mulungu ananena chomwecho, Izo zikukhazikitsa ichi.”

⁵⁸² Abrahamu, kwa yemwe lonjezolo linaperekedwa, kwa iye ndi Mbewu yake, iye anazitcha zinthu zomwe panalibe, ngati kuti zinalipo. Pakuti, Ilo linali lonjezo la Mulungu, podziwa kuti Mulungu sangathe kunama. Iye anamulonjeza iye zimenezo, ndipo iye anazikhulupirira Izo. Ndipo pamene zaka zinkadutsa apo, ndipo lonjezolo linkawoneka ngati liri kutali kwambiri, kwa diso lachibadwa, Ilo linkakhala loyandikirapo kwa Abrahamu.

⁵⁸³ Mmaloti moti akhale wofooka, nkuti, “Chabwino, mwinamwake palibe chinthu choterocho ngati machiritso Auzimu. Mwinamwake ine ndinalakwitsa kuyankhula. Mwinamwake palibe chinthu choterocho. Mwinamwake ine ndakhala ndikulakwitsa mu malingaliro anga onse.” Ndiye, izo zikusonyeza chinthu chimodzi, kuti inu simunabadwe kachiwiri. “Pakuti ndi . . .”

⁵⁸⁴ Ife tinadutsamo Lamlungu lapitali, kupita pang’ono pokha mmbuyo mu mutu. “Pakuti ndi kosatheka kwa munthu yemwe anayamba walawapo mphatso Zakumwamba ndi zinthu, kuti agwere kutali, ndi kudadzikonzanso yekha mwa kulapa.” Mwamtheradi, kwathunthu nzosatheka!

Pakuti iye amene *wabadwa mwa Mulungu samachita* ndipo sangakhoze *kuchita tchimo; pakuti mbewu ya* Mulungu imakhalabe ili *mwa iye: ndipo iye sangakhoze kuchimwa, . . .*

Mbewu ya Mulungu ndiyo Mawu a Mulungu. “Chikhulupiriro chimadza pa kumva, kumva Mawu, ‘Nsembe inapangidwa. Izo zonse zatha.’”

⁵⁸⁵ Tsopano, ngati inu muchita molakwitsa, Mulungu akupangitsani inu kuti mulipire pa izo. Koma ngati inu mutero,

inu mwalakwitsa, inu simumachita izo mwakufuna. Mutu wa 10, ndime ya 47, ine ndikukhulupirira, “Pakuti ngati ife tichimwa mwadala ife titalandira kale chidziwitso cha Choonadi.” Koma iwe ukakhala Utabadwa kale, iwe umakhala nacho Choonadi; osati chidziwitso cha Icho, koma iwe wachivomereza Choonadicho ndipo Icho chakhala chenicheni. Ndipo ndiwe mwana wa Mulungu, kwa nthawi ndi Muyaya. Mulungu analumbira kuti Iye akanadzachita izo.

⁵⁸⁶ Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo Ine ndidzamuutsa iye pa tsiku lotsiriza. Iye sadzabwera konse ku chiweruzo. Iye wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Tsopano ndi lumbiro long a limenelo, “Mulungu akulolela kuti ife tizililandira Ilo.”

⁵⁸⁷ Tsopano penyani zomwe iye akunena apa, Paulo akuyankhula kwa—mpingo.

...ndi *kosatheka kuti Mulungu aname, ife tiyenera kuti tikhale ndi chithonhozo champhamvu,...*

Osati, “Chabwino, ngati Abaptisti sazindichitira ine mwabwino, ine ndipita kwa Amethodisti.” Mukuona?

...ife *tikuyenera* kukhala ndi chithonhozo champhamvu, *amene tathawa pofuna pokabisala kuti tigwire pa chiyembekezo chaikidwa patsogolo pathu:*

⁵⁸⁸ Tsopano mu kuwerenga kwa yotsiriza.

Chiyembekezo chomwe ife tiri nacho ngati nangula wa moyo,...

Chiyembekezo, lumbiro lolumbiridwa la Mulungu, ife tiri nalo ngati nangula wa moyo, palimodzi chokhazikika ndi cholimba, ndi omwe alowa mkati umo ali mkati mwa chophimba;

⁵⁸⁹ Tiyeni tiyankhule mphindi yokha pa “chophimba.” Ife sitinazitenge izo mwabwino momwe Lamlungu lapitali usiku.

⁵⁹⁰ “Mu chophimba.” Chophimbacho ndi mnofu. Chophimba ndi chimene chimatilepheretsa ife kuti tisamamuone Mulungu, maso ndi maso, mu mpingo uno. Chophimba ndi chimene chimatiletsa ife kuti tisawawone Angelo pa malo awo mma uno, ataima pafupi ndi mipando. Chophimba ndi chimene chimalipheretsa ife kuti timuwone Iye. Ife tabisika kuseri kwa chophimba, ndipo chophimba chimenecho ndi mnofuwu. Ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, ife tiri mu Kukhalapo kwa Mulungu, “Angelo a Mulungu akuzungulira pa iwo amene amamuwopa Iye.” Ife tiri mu Kukhalapo kwa Mulungu, nthawi zonse. “Ine sindidzakusiyani konse inu, ngakhale kukutayani inu. Ine ndizikhala ndi inu nthawizonse, ngakhale mpaka kumapeto.” Koma chophimba ndi mnofu, ndi chimene chimatitchinga ife kutichotsa mu Kukhalapo kwa Iye. Koma

kupyolera mmoyo, Mzimu, mwa chikhulupiriro chatu ife timadziwa kuti Iye akutipenya ife. Iye waima pafupi nafe. Iye ali pano tsopano.

⁵⁹¹ Kuja ku Dotani, mmawa wina, mneneri wachikulire anazunguliridwa ndi ankhondo ndipo wantchito wake anapita panja ndipo anati, “O bambo, dziko lonse lazunguliridwa ndi akwina.”

⁵⁹² Ndipo Eliya anauka apo, ndipo anati, “Pakutitu, mwananga, pali ochuluka omwe ali ndi ife kuposa omwe ali ndi iwowo.”

⁵⁹³ Chabwino, iye anaphethira maso ake ndipo anayang’ana pozungulira. Iye sankakhoza kuwona kena kalikonse.

⁵⁹⁴ Iye anati, “Mulungu, ine ndikanafuna kuti Inu mumutsegule maso ake, mumuchotsere chophimbacho.” Ndipo pamene chophimbacho chinagwa nkuchoka pamaso ake, momuzungulira mneneri wachikulire uja panali agaleta a moto, mapiri anali pa Moto ndi Angelo ndi magaleti. Ndi inu apo.

⁵⁹⁵ O, ndiye Gehazi akanakhoza kunena kuti, “I—ine ndikumvetsa tsopano.” Mukuona, chophimba chinakanganukapo. Apo ndi pamene pali cholepheretsa.

⁵⁹⁶ Ndi izi apa. Zigwireni izi molimba. Chophimba ndi chimene chimatilepheretsa ife kuti tisamakhale momwe ife timayenera. Chophimba ndi chimene chimatilepheretsa ife kuti tisamachite zinthu zomwe ife timafuna kuti tizizichita kwenikweni. Ndipo Mulungu anadzaphimbidwa mu mnofu, ndipo chophimbacho chinang’ambidwa pawiri. Ndipo Mulungu anakhala Mulungu kachiwiri, ndipo Iye anachiukitsa chophimba chomwe Iye ankadzibisamo Iyemwini. Ndicho chiwukitsiro cha Ambuye Yesu. Kutsimikizira kwa ife kuti, mu chophimba ichi chomwe ife tabisalamo tsopano, mwa chikhulupiriro ife timakhulupirira Izo ndi kuvomereza Izo. Ndipo pamene chophimba *ichi* chidzang’ambidwa pawiri, ine ndidzapita mu Kukhalapo Kwake ndi chitsimikizo ichi, podziwa kuti, “Ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake.” Pa Kudza kwa Ambuye Yesu, chophimba ichi chidzaukitsidwad aponso, mwa njira yangwiro, mpaka ine ndizidzayenda ndi kumayankhulana ndi Iye monga Mpulumutsi wanga ndi Mulungu wanga, pamene Iye adzatenga mpandowachifumu wa Davide. Ndipo ife tizidzakhala moyo kwanthawizonse mu chophimba ichi chitapangidwa kukhala changwiro, koma chophimba ichi chiri ndi tchimo mwa icho. Izo ziribe kanthu momwe. . . Musati muziganiza konse za thupi laulemerero ilo mu dziko ili. Ili liyenera lidzafe, mofanana monga solo yanu iyenera kuti ife, kuti mubadwe kachiwiri.

⁵⁹⁷ Mu ungwiro, kusadya nyama, ndi kuchita *izi*, ndi kulipangitsa thupi kukhala langwiro, inu simudzakhala nazo Izo konse. Ndipo inu muyenera kusiya *izi*, ndi kuchita *izi*, ndi kuchita *izi*, ndi kuchita *izi*, ilo ndi lamulo. Ndiwo azamalamulo. Ife sitimakhulupirira mu mtundu wamalamulo

wa chipulumutso. Ife timawakhulupirira Iwo kuti mwa chisomo ife tinapulumsidwa. Ndipo si inuyo. Inu munalibe kanthu kochita ndi zimenezo. Ndi kusankha kwa Mulungu komwe kumachita izo. “Palibe munthu angadze kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye.” Ndiko kulondola. Ndipo Iye... Zonse zomwe Yesu anabwera kuti adzachite kunali kuti adzawatenga awa omwe Atate anawadziwiratu; ndipo anawakonzeketsera iwo asanaikidwe maziko a dziko. Iwo amadzakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ameni. “Si iye yemwe athamanga, kapena iye amene afuna, koma Mulungu yemwe amasonyeza chifundo.” Mulungu ndi yemwe amachita izo. Inu simungadzibwekerere, nkomwe. Palibe kanthu komwe inu munakachita. Mulungu, mwa chisomo, anakupulumutsani inu; osati inu, inueni. Ngati inu mutatero, inu muli nacho chinachake choti muzidzibwekerera nacho. Koma inu mulibe kanthu koti muzidzibwekerera nako. Matamando onse amapita kwa Iye. Ndi Iyeyo. Ndiye Iye wakupatsani inu chiyembekezo chotsimikizika, “Analumbira pa lumbiro, kusatheka koti ana ake ataike konse.”

⁵⁹⁸ Tsopano, iwo amakwapulidwa chifukwa chochita zolakwika. Inu mumakolola zomwe inu munabzala. Inu mumvetse izo. Musati muziganiza tsopano kuti inu muzingopita ndi kumakachimwa, ndi kumadutsa nazo izo. Ngati inu mutero, ndipo ndikukhala ndi lingaliro limenelo, izo zizisonyeza kuti inu simunayambe mwabadwa mwatsopano. Inu mukuzimvetsa izi? Ngati inu muli nachobe chikhumbo mwa inu, kuti muzichita zolakwika, ndiye inu mukadali wolakwika. Mukuona? “Pakuti Iye watikhaliisa ife angwiro, kwanthawizonse, iwo omwe ali... Ndipo zinyama zija pansu pa Chipangano Chakale, pansu pa masiku alamulo, zinkaperekedwa pachaka, mopitirira, sizikanakhoza konse kulichotsa tchimo.” Koma pamene ife tiyika manja athu pa mutu Wake, ndi kuvomereza machimo athu ndi kukhala titabadwa mwatsopano mwa Mzimu wa Mulungu, ife sitimakhalanso ndi chikhumbo china cha tchimo. Tchimo lachoka kwa inu. Izo ndi kwa kwanthawi ndi Muyaya.

⁵⁹⁹ Inu muzipanga zolakwitsa. Inu muzigwa. Inu muzilakwitsa mwadala. Inu muzituluka nthawizina ndi kukachita zinthu. Izo sizikutanthauza kuti inu mwataika. Izo zikutanthauza kuti inu mulandira kukonzedwa.

⁶⁰⁰ Mnyamata wanga wamng’ono, nthawi zambiri, ana anga, amachita zinthu. Anu amatero, nawonso. Zomwe inu... Iwo amadziwa kuti izo ndi zotsutsana ndi malangizo a—anu. Ndipo iwo amadziwa choti achiyembekezere pamene iwo achita izo. Iwo apeza kukwapulidwa chifukwa cha izo, nthawizina kwabwino komwe. Koma iye akanali mwana wanu. Ndithudi.

⁶⁰¹ Ndi kosatheka kuti munthu ameneyo adzakhale atapita kachiwiri, yemwe nthawiina anayamba wabadwa ndi Moyo Wamuyaya. Mulungu si wopereka mwa Chimwenye. “Iye amene

amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha; ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo. Ine ndidzamuutsa iye mu masiku otsiriza.” Ndilo lonjezo la Mulungu.

⁶⁰² Tsopano ngati inu muzipitirira, ndi kumati, “O, chabwino, ndiye ine ndikhoza kuchita basi...” Ine nthawizonse ndimachita zomwe ine ndimafuna kuti ndizichita. Koma ngati iwe uli Mkhristu, iwe sumafuna kuti uzichita zinthu zomwe ziri zolakwika, chifukwa Moyo womwe uli mwa iwe, maziko omwe. Ngati iwe ukufuna kuti uzichita zolakwika, izo zikusonyeza kuti muli chinthu cholakwika mkati *umu*. “Zingatheke bwanji kuti madzi oipa ndi okoma azichokera pa kasupe yemweyo?”

⁶⁰³ Chotero inu mwakhala yense wosokonezeka, pa mtundu wina wa kutengeka kapena chinachake chopambana, kugirigisha kwinakwake. Iwalani izo. Bwererani ku guwa ndi kukati, “Mulungu, uchotseni moyo wanga wakale wamachimowu, ndi kundiika ine mu chikhalidwe chotero kuti chikhumbo changa chonse...”

“Iye amene ali wobadwa mwa Mulungu samachita tchimo.” Uko nkulondola. Iye alibe chikhumbo choti azichita chotero.

⁶⁰⁴ Ndithudi, Mdierekezi azimutchera iye msampha *apa* ndi *apo*, koma osati mwadala. Baibulo linanena chomwecho. Mdierekezi azimutchera iye msampha, pano ndi apo. Zedi, iye azitero. Iye anayesera kuti aponyere misampha kwa Ambuye wathu Yesu. Iye anatero kwa Mose, ndipo anamukola iye. Iye anatero kwa Petro, ndipo anamukola iye. Iye anachita kwa ambiri. Koma Petro ngakhalenso anamukana Iye, koma ndiye iye anapita ndipo anakalira mowawidwa. Munali chinachake mwa iye.

⁶⁰⁵ Pamene nkhunda inatulutsidwa mu chombo... Khwangwala anapita kunja, iye ankabwekerera konseko. Iye anali mu chombo bwino bwino, koma pamene iye anapita kunja, chikhalidwe chake chinali chosiyana. Iye ankakhoza kudya nyama zonse zakufa momwe iye ankazifunira, ndi kumakhutitsidwa. Bwanji? Iye anali khwangwala, pakuyamba pomwe. Iye anali nkankhaziwisi. Iye anali wopanda ubwino. Iye anali wachinyengo yemwe anakhala pa chisa limodzi ndi nkhunda, wamkulu basi monga momwe nkhunda inaliri. Iye ankakhoza kuwulukira kulikonse komwe nkhunda inkakhoza kuwulukira. Koma iye akanakhoza kudya zakudya zabwino monga momwe nkhunda imadyera. Ndiyeno iye akanakhoza kudya zakudya zovunda, zomwe nkhunda sikanakhoza kuzidya. Pakuti, nkhunda ndi kusakaniza kosiyana. Iye ndi wopangidwa mosiyana. Iye ndi nkhunda. Ndipo nkhunda singakhoze kugaya chakudya chovunda, chifukwa iyo ilibe ndulu iliyonse.

⁶⁰⁶ Ndipo munthu yemwe ali wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu amakhala nkhunda ya Mulungu, chikhalidwe chake, kusintha

kwake, mapangidwe ake. Inde, bwana. Inu muike mzimu w—wa nkunda mwa khwangwala, iye sangakhalenso konse pa nyama yakufa. Ngati iye ataterapo mwangozi, iye angayese kuti achokepo mofulumira. Iye sangakhoze kuzipirira izo. Ndipo munthu yemwe wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, samakhala wosalekerera. Iye akhoza kutera mu nyumba yamowa nthawiyina, koma iye achoka mmenemo mofulumira. Mkazi akhoza kumudolola iye, ndi kumupangitsa iye kutembenukira kumeneko, koma iye apotoloza mutu wake kachiwiri. Iye achoka ku zimenezo mofulumira. Bwanji? Iye ndi nkunda. Ndiko kulondola. Inu simuti mumupusitse iye, chifukwa kuti iye amadziwa. “Nkhosa zanga zimadziwa Liwu Langa, ndipo mlendo izo zizingamutsatire.” Iye ndi nkunda, pakuyamba pomwe. Ndi zomwe ine ndikuzinena, chinachake chenicheni chimene chimazika mkati umo.

⁶⁰⁷ Penyani mwatcheru tsopano. “Mulungu analumbira.” O, izo. . .

Chiyembekezo chomwe ife tiri nacho ngati nangula wa solo, zonse . . . chokhazikika, ndi chimene chimalowa m—mu icho chomwe chiri chophimba;

⁶⁰⁸ “Chophimba.” Mulungu anabwera pansi, ataphimbidwa mu mnofu. Kutu achite chiani? Kutu adzisonyeze Iyeyekha. Iye ankachita kubisala, chifukwa ife sitikanakhoza kumuwona Iye. Ndipo Iye ankabisala kuseri kwa chophimba. Ndipo chophimbacho chinali ndani? Yesu. “Si Ine yemwe ndikuchita ntchitozi, Atate Anga,” anatero Yesu. “Atate Anga akukhala mkati Mwanga. Ine ndikugwira ntchito. Atate akugwira ntchito, ndipo ine ndikugwira ntchito pa zomwezo.” Apa Iye ali monga wophimbidwa Uyo, akuyenda mu mnofu, Mulungu, Emanuele, Mulungu nafe. “Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini.” Apa Iye ali, akuyendayenda.

⁶⁰⁹ Tsopano, Iye anabwera pansi ndipo anadzapanga chiyeretso, kapena njira, kapena chitetezero, kuti kupyolera mu imfa Yake anapereka, analipira mtengo wa tchimo, kuti Iye adzakhoze kubwereranso ndi kudzakhala mkati mwa ife. Ndiye chikhulupiriro chomwe ife tiri nacho n—ndi chikhulupiriro chophimbidwa, kapena munthu wophimbidwa. Chotero ife sitimayang’ana pa zinthu zomwe ife timaziwona mu chophimba ichi. Chophimbachi chiri ndi maphunziro, ndipo icho chimachita zinthu ndi kuyankhula zinthu. Ndi chinthu chasayansi. Koma Mzimu wa Mulungu wamoyo umene umakhala mkati umu, umazitcha zinthu izo zomwe palibe, ngati kuti izo zilipo, ngati Mulungu wanena chomwecho. Ndi uko kuphimba kwanu. Iye tiri mu chophimba.

⁶¹⁰ Tsopano, tsikulina Iye adzachiwukitsa chophimba ichi, osati chobadwa ndi mkazi mwa chikhumbo chakugonana kwa mwamuna ndi mkazi, koma mwa chifuniro cha Mulungu

Iye adzayankhula ndipo iye adzakhhalapo. [M'bale Branham anakhwatchitsa chala chake—Mkonzi.] Ndiye ife tidzakhala nalo thupi longa thupi Lake lomwe laulemerero. Ife tidzaphimbidwa, chotero kuti ife tizidzakhoza kuyankhulana kwa wina ndi mzake, kugwirana chanza wina ndi mzake.

611 Tsopano, pamene ife tidzapita kuchokera kuno, pali kachisi, fiofane, fano chabe la munthu, lomwe silimadya, silimamwa, silimagona, logalamuka kwanthawizonse. Uko ndi kumene ife tikupitako. Koma iwo akudikirira pansi pa Guwa, akufuula, “Ambuye, mpaka liti? Mpaka liti?” kuti tibwerere pansi. Chifukwa, iwo akufuna azigwirana chanza wina ndi mzake. Iwo akufuna kuti azikhala pansi ndi kumadya, ndi kuyankhulana kwa wina ndi mzake. Iwo ndi anthu. Lodala likhale Dzina la Ambuye!

612 Pamene Mulungu anamupanga munthu mu chifanizo Chake chomwe pachiyambi, Iye anamupanga iye chotero. Iye ankachita chiyanjano kwa wina ndi mzake, chifukwa ife tikudziwana wina ndi mzake. Ife timazikonda zinthu zomwe Mulungu anatipanga ife, chifukwa ife tinapangidwa chotero. Mu Kudza Kwake kwakukulu, omwe ali okonzeka adzakhala chotero kwanthawizonse. Achisavundi, ife tidzaima mofanana Naye. O lidalitsike Dzina ilo la Khristu!

613 Ndipo tsopano ife tiri nacho chikole cha chipulumutso chatu, pamene ife timuvomereza Iye, monga Mpulumutsi wathu, monga mchiritsi wathu. Zolandira zina zonse izi ndizo phindu lomwe linaperekedwa pa dongosolo la inshuranse. Amen. Inu mukudziwa chomwe dongosolo la inshuranse liri. Inu mukhoza kutenga zopindula pa iyo kufikira mtengo weniweni utabwera. Ndithudi. Inu mukhoza kutengapo zopindula. Ndipo ife tikutenga zopindula pano. Kokha, chinthucho, mwamsanga pamene ife titenga zopindula, zolandirazo zimachulukamonso.

614 Wogulitsa inshuranse, nthawi ina, anati kwa ine, “Billy, ine ndikufuna kuti ndikugulitse iwe inshuranse.”

Ine ndinati, “Ine ndiri nayo ina.” Akazi anga anayang’ana motembenukira kwa ine.

615 Tsopano, ndiribe chotsutsa inshuranse. Koma anthu ena ali ndi “inshuranse akusauka.” Chotero, iwo anatembenuka apo. Iye anati. . .

616 Akazi anga anandiyang’ana ine, mwachilendo. “Iwe uli nayo inshuranse?”

617 Ine ndinati, “Zedi.” Iye sankadziwa kanthu za iyo.

618 Iye anati, “Chabwino, Billy, ndi mtundu wanji wa inshuranse yomwe uli nayo?”

619 Ine ndinati:

Chitsimikizo chodala, Yesu ndi wanga!
 O, kulawiratu kwake kwa ulemerero Wauzimu!
 Wolandira chipulumutso, wogulidwa ndi
 Mulungu,
 Wobadwa mwa Mzimu Wake, wotsukidwa mu
 Magazi Ake.

⁶²⁰ Iye anati, “Izo ndi zabwino kwambiri, Billy,” iye anati, “koma iyo siidzakakuika iwe kuno mmanda.”

⁶²¹ Ine ndinati, “Koma Iyo idzanditulutsamo ine. Ndicho chinthu chofunikira.” Ine sindikudandaula za kulowa mmenemo; ine ndikudandaula za momwe ndingatulukiremo.

⁶²² Ndipo pakuti ine ndiri nacho chitsimikiziro, mwa kulumbira kwa Mulungu Wamuyaya, kuti Iye adzandiukitsanso ine mu mawonekedwe a Mwana Wake, mu tsiku lotsiriza, ine ndiziyenda molimba mtima ndi kukhala nacho chithonhozo ndi nangula wa moyo, kuti, pamene ine ndikadali mu chophimba ichi pali Chinachake chosawoneka chomwe chinandizika ine pa Thanthwe la mibadwo kutaliko. Pamene madzi alumpha ndi kuwomba, izo sizimapanga kusiyana kulikonse. Ngati imfa, zowopsya, kapena chirichonse, sizingatilekanitse ife ku chikondi cha Mulungu. Nangula wanga wagwira mkati mwa chophimba. Siyani madzi azisefukira. Asiyeni iwo azigunda. Asiyeni achikunja azibwera. Wokhulupirira wobadwa kachiwiri ali ndi nangula. Inu simukukhoza kupenya kupyolera mu chophimba ichi panobe. Koma ine ndikudziwa nangula wanga wagwira kutaliko pa Thanthwe la mibadwo, Yemwe ali lonjezo lolumbiridwa kuti Iye adzandiukitsa ine pa tsiku lotsiriza.

⁶²³ Palibe zodabwitsa inu mukhoza kuiyang’ana imfa mu nkhope, nkuti, “Mbola yako ili kuti? Manda, chigonjetso chako chiri kuti? Koma zikomo akhale kwa Mulungu yemwe amatipatsa ife chigonjetso kudzera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” Ife tiri mu Wotsogolerakudza. O, mai! (Ife sitifika ku phunziroli.) Ife tinali naye Wotsogolerakudza kwa ife.

⁶²⁴ Wotsogolerakudza. Kodi inu munayamba mwazindikira mu masiku akale a akumadzulo. Nthawi zambiri ine ndadutsapo mu tinjira takale. Wotsogolerakudza, kapena wokafufuza? Pamene gulu la ngolo linali kutha, posowa madzi, wokafufuza ankathamangira patsogolo. Ndipo iye akawona mafuko a Achimwenye; iye ankawalambalala iwo. Ndipo iye akawona pamene panali kasupe wa madzi. Iye ankathamangira mmbuyo kuti akamuuze bwana wa gulu la ngolozo, “Ikani zishalo akavalowo, aliyense atenge kulimbika kwabwino, pakuti kuseri chabe kwa phirilo kuli kasupe wamkulu wa madzi.” Iye ndi wotsogolera kudza.

⁶²⁵ Ndipo apa, Wotsogolerakudza. Munthu anayamba wakanikizidwirapo pansu ndi Mdierekezi, pansu pa moto waukulu, koma Winawake anatenga chisa cha makina

a mfuti. Ameneyo anali Yesu. Wotsogolerakudza anapita patsogolo pathu. Ndipo Satana ataima pamenepo ndi mfuti ya makina, akutikanikizira ife pansi, nthawizonse mu msinga ndi kumaiwopa imfa. Iye anali akulondera Kasupe ameneyo. Zedi, iye anali. Iye anapatsidwa udindo, chifukwa ife tinali titachimwa ndipo tinali titathamangitsidwira kutali ndi Iye. Koma Wotsogolerakudza, Khristu, anabwera umo ndipo anadzachitenga chisacho.

⁶²⁶ Inu munaimvapo nyimbo yakale ija, “Gwirani linga, pakuti ine ndikubwera”? Gwirani linga, mopanda kupereze; tiyeni tizitenge izo. Iye sitikufuna kuti tigwirensa izo motalika. Khristu analitenga lingalo. Aleluya! Chitseko ndi chotseguka. “Pali Kasupe wotseguka mu nyumba ya Mulungu, mu mzinda wa Davide, kuti ayeretse, wa kuyeretsa kwa osayera.” Wotsogolerakudza wathu analowa kale umo mmalo mwa ife.

⁶²⁷ Wotsogolerakudza, Iye akutiiza ife, “Alipo malo kutsidya, kutaliko, komwe inu simudzakhala okalamba.” Komwe sikudzakhalanso makwinya, komwe simumadzachita kumadzagwiritsa ntchito Max Factors kuti akupangitseni inu kumawoneka bwino kwa amuna anu. Wotsogolerakudza wapita kale. Kulibeko malo omwe inu mungati mukakalambe ndi kufooka ndi kunjenjemera. Alipo malo omwe inu simudzakadwalako konse. Komwe mwana sadzakakhala konse ndi ntchirikilo. Komwe inu simudzakataya konse loikirira. . . kapena dzino, kuti muikiremo lonamizira. Aleluya! O lodala likhale Dzina Lake! Iye anakalowa umo, ndipo mwa chisavundi ife tidzakaima mofanana Naye, tsiku lina kutaliko. Nyenyezi ndi dzuwa izo zidzawala mopedwa. Ndithudi. Wotsogolerakudza anapita patsogolo pathu.

*. . . wotsogolerakudza anapita, anatilowera ife,
ngakhale Yesu, anapangidwa wansembe wamkulu kwa
nthawizonse mwa dongosolo la Melkizedeki.*

⁶²⁸ Wotsogolerakudza wamkulu uyu anapita patsogolo pathu, kutikonzera njira. Iye anakhala kuchokera pa mzimu, akasupe aakulu a utawaleza wa Mulungu, yemwe analibe chiyambi kapena mapeto. Iye anali, kwanthawizonse, Mulungu.

Mlozo uwu wa Kuwala unapita apo. Iwo unali mlozo wa chikondi, ndiwo waukulu wake, wofiira. Mtundu wotsatira unatsatira, womwe unali wa buluu; buluu, kuona. Wotsatira, umene unatsatira pambuyo pa iwo inali mitundu inayo, kudutsa mitundu isanu ndi iwiri yangwiro, yomwe ili mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu, yomwe inapita kuchokera ku Kasupe wamkulu kapena Daimondi wamkulu yemwe Yesu anamukamba. Daimondi wamkulu uja anadulidwa, kuti anyezimiritse mitundu imeneyi. Mulungu anapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu, kuti Iye akhoze

kumanyezimiritsa ubwino Wake ndi chifundo pakati pathu, mwa mphatso ndi zizindikiro ndi zodabwitsa.

Utawaleza wonse wawukulu uja unadzakhala mu fiofane, unapangidwa mu chifanizo chonga cha munthu. Komabe, Iye sanali munthu; Iye analibe mnofu, apabe. Iye anali fiofane.

⁶²⁹ Mose anati, “Ine ndikanafuna kuti ndikuwoneni Inu.” Mulungu anamubisa iye mu thanthwe.

⁶³⁰ Ndipo pamene Iye ankadutsa apo, Iye anapotolozwa nsana Wake. Mose anati, “Two unawoneka ngati nsana wa munthu.”

⁶³¹ Ndiye chinadzachitika ndi chiani? Tsiku lina kumusi uko, pamene Abrahamu anali atakhala mu hema wake. Iye tifika kwa izo, usikuuno. Pamene Abrahamu anali atakhala mu hema wake, Mulungu anabwera uko kwa iye, mu thupi la mnofu.

“O,” inu mukuti, “M’bale Branham, iye anali . . .”

⁶³² Iye timupeza Iye kunjwa uku akukomana ndi Abrahamu zisanachitike zimenezo, mu dongosolo la Melkizedeki, thupi la mnofu, lomwe linali Mulungu. Zedi, uyo anali. Iye anali Mulungu mu thupi.

⁶³³ Inu mukuti, “Ndiye, M’bale Branham, chifukwa chiani Iye anachita kubweranso ndi kudzabadwa?”

⁶³⁴ Iye anali asanabadwe pa nthawi imeneyo. Iye anangochita kulengedwa, thupi lomwe Iye ankakhalamo. Melkizedeki anali Mfumu ya Salemu, yemwe ali Mfumu ya Yerusalemu, yemwe anali Mfumu ya mtendere; yemwe analibe ngakhale abambo kapena amayi, kuyamba kwa masiku kapena mapeto a moyo.

Yesu anali nawo onse abambo ndi amayi, ndi chiyambi cha masiku ndi kutha kwa moyo. Koma Iye anapangidwa “monga mwa dongosolo” la Melkizedeki, yemwe analibe chiyambi cha masiku kapena kutha kwa moyo.

⁶³⁵ Melkizedeki anali Mulungu Iyemwini. Melkizedeki anali Yehova Mulungu, Yemwe uja amene anakomana ndi Abrahamu, zaka zamtsogolo, kumaso kwa hema wake. Anali ndi nsana wake atautembenezira kwa iye; Iye anati, “Bwanji Sara anaseka?” Ndiko kulondola. Iye anali Mmodzi yemwe anaima pamenepo, akuyang’ana chaku Sodomu. Abrahamu anamuzindikira Iye, chifukwa mkati mwa chophimba chake munali nangula ataligwira lonjezo lija. Osati chifukwa chakuti iye anali ndi kumverera kwina, koma Mulungu anamupangira iye lonjezo. Ndipo pamene iye anafika pokhudzana ndi maginito aakulu amenewo, iye anadziwa kuti Iyo inali mu mnofu Umenewo.

⁶³⁶ Anayenda napita limodzi ndi Abrahamu, kunjwa uko kantunda kakang’ono. Iye anamuza Abrahamu. Anati, “Nditawona izo, Ine ndimubisile Abrahamu zinthu izi, powona kuti iye ndi wolandira dzikoli? Ine sindingachite basi zimenezo.” Chotero, “Abrahamu, Ine ndikuuza iwe chimene Ine ndikukachita pa ulendo Wanga,” ife tizitenga izo

usikuuno, “akupita uko ku Sodomu,” ndi zomwe iwo onse anali kuti akachite. Ndipo mwamsanga pamene Iye anamudalitsa Abrahamu, Iye anapita nabwerera mu danga kachiwiri. Bambo yemwe anaima pamenepo ndipo anali ndi fumbi pa zovala Zake, munthu. Ndipo osati icho chokha, koma Iye anadya nyama ya ng’ombe yaing’ono yomwe Abrahamu anaipha, ndipo anamwa mkaka wochokera ku ng’ombe yaikazi, ndi kudya zitumbuwa zina (zikondamoyo zina), ndipo anaika batala pa izo. Ndiko kulondola ndendende. Ndiyeno anatembenuka nabwerera ku fiofane kachiwiri.

637 Kodi chinali chiani icho? Bwanji Iye sanalitenge ilo apo? Iye anali asanachite kubadwa monga inu ndi ine. Koma Iye ankayenera kuti adzachite kubadwa mu mnofu, chotero kuti Iye adzakhoze kuigwira mbola ija. Lijali linali thupi lochita kulengedwa. Lijali linali thupi lomwe Iye anangokoka kashiamu ndi potashi kuchokera pa dziko lapansi, ndipo anati, “Pfyuu,” ndipo analowa mu ilo. Icho chinali chinthu chomwecho chimene Melkizedeki anali. Iye analowa mwa iye, mu thupi lomwe Iye akanakhoza kumayenda nalo patsogolo pa iye pansu pa chophimba, chophimba cha chilengedwe Chake chomwe; osati chophimba cha chirengedwe cha mkazi, kupyolera mu chiberekero cha mkazi, kupyolera—mu khungu, ayi. Koma Iye analilenga ili ndipo anadzalowa mu ilo, ndipo ankayankhula, mwa dongosolo la Melkizedeki.

638 Kodi Melkizedeki uyu ndi ndani?

Pakuti Melkizedeki uyu, mfumu ya Salemu, (yomwe ili Yerusalemu), kalonga wa Mulungu wammwambawamba, ndithudi, yemwe anakomana ndi Abrahamu akubwerera kuchokera kokapha mafumu, ndipo anamudalitsa iye;

Kwa yemwenso Abrahamu anapereka gawo la khumi la zonse; poyamba pokhala mwa kutanthauzira Mfumu ya chilungamo, (chikondi chachikulu chija, chikondi, Mzimu wawukulu uja pachiyambi)...Mfumu ya chilungamo, ...pambuwo pake...Mfumu ya Salemu, yemwe ali, Mfumu ya mtendere;

Wopanda bambo, wopanda mayi, wopanda kochokera, ali wopanda ngakhale chiyambi cha masiku, kapena mathero a moyo; . . .

639 Anali ndani ameneyo? Iye sanachite kubadwa konse, Iye sadzafa konse. Ndi ndani ameneyo? Iye anali Mulungu, zedi, iye anali, mwa mthunzi woyambirira wa Ambuye Yesu. Ndithudi anali. Koma Iye anachita kubwera kudzera mwa mkazi, mwa dongosolo lomwe inu mumadzera kupyolera mwa mkazi. Ndipo Iye ankayenera kuti abwere mwanjira yomwe inu mumadzera, mwa cholinga chakuti akubwezeretseni inu kwa Iye. Aleluya!

Chisomo chodabwitsa, kukoma kwake
 kuchimva,
 Chimene chinapulumsa wosauka,
 wopandapake wakhungu ngati ine!
 Ine poyamba ndinali wotaika, koma tsopano
 ndapezeka, mwa chisomo Chake,
 Ine ndinali wakhungu, koma tsopano ine
 ndikupenya.

⁶⁴⁰ Ine ndikumvetsa zomwe Iye ankayenera kuti azichite. Mulungu anadzakhala ine, kuti ine mwa chisomo ndikhoze kukhala Iye. Iye anatenga machimo anga, kuti kupyolera mu chilungamo Chake ine ndikhoze kukhala nawo Moyo Wamuyaya. Ine sindikanakhoza kudzisankha ndekha. Chikhalidwe changa chinali wochimwa. Ine ndinalibe kanthu koti ndichite ndi izo. Ine “ndinabadwa mu dziko, ndinaumbidwa mu kusaweruzika, ndinabwera mu dziko kumayankhula bodza.” Ndiliba ngakhale mwayi, konse; palibe kalikonse, opanda ngakhale chikhumbo.

⁶⁴¹ Iwuzeni nkhumba “ikulakwitsa, pomadya zammatope,” mungatero inu? Muwone kuchulukwa kwa momwe iyo ingakumvereni inu. Muwuzeni khwangwala iye “akulakwitsa, pakumadya pa nyama yakufa,” ndi kuwona zomwe iye atakuuzeni inu. Ngati iye akanakhoza kuyankhula, “Iwe zisamala ntchito ya iwe wekha.” Ndithudi.

⁶⁴² O, koma chisomo cha Mulungu chimene chinasintha chibadwa ichi, ndi kundipatsa ine mwayi kuti ndizikhumba ndi kumalalakala ndi kuchita ludzu, “Chikondi chanu, chifundo, ndi chabwino kwa ine kuposa moyo, O Mulungu. Mtima wanga ukukhala ukukhumba kufuna Inu.”

⁶⁴³ Davide anati, “Monga mbawala ipuma wefuwefu kufuna khwawa la madzi, chomwechonso moyo wanga ukuchita ludzu kufuna Inu, O Mulungu.”

⁶⁴⁴ Mulungu anamupatsa munthu ludzu limenelo, kuti azimupembedza Iye, kuti azikonda, kumufunafuna Iye. Koma munthu amazipotoza izo mwa kuitanira kwa Mdierekezi, ndipo iye amapita ndi kumakawasilira akazi ndi zosangalatsa ndi zinthu za mdziko, poyesera kuti akhutitse chilengedwe choyera icho chimene Mulungu waika umo, kuti azimukonda Iye. Iye amachiika icho pa zinthu za mdziko. Koma, m'bale, pamene iye angosintha kamodzi, ndipo kasupe uyo yemwe ali ndi tovinita michira mwa iye, mitundu yonse y—ya zosoknezeka za chitsimecho, zatsukidwamo ndi kutenthedwa, ndipo Madzi angwirowo a Mulungu ayikidwa mmenemo, tchimo silingakhoze kuzikhudza izo. Amen.

O momwe ine ndimkondera Iye! Momwe ine
 ndimyamikira Iye!
 Moyo wanga, dzuwa langa, zonse wanga mu
 zonse!

Mlengi wamkulu anakhala Mpulumutsi wanga,
Ndipo chidzalo chonse cha Mulungu chiri mwa Iye.

Kutsika kuchokera ku ulemerero Wake, nkhani ya moyo yokhayo,
Mulungu wanga ndi Mpulumutsi anadza, ndipo Yesu linali Dzina Lake.

Anabadwira mu khola, kwa Ake omwe mlendo,
Mulungu wazisoni, misozi ndi zowawa.

O momwe ine ndimkondera Iye! Momwe ine ndimyamikira Iye!

Mpweya wanga, dzuwa langa, zonse wanga mu zonse!

⁶⁴⁵ O Mulungu! Iye akanakhoza kuchita motani izo? Munthu anayeserapo kuzilemba izo. Wina anati:

Ngati ife tikanakhala ndi kapezi wodzaza nyanja,
Ndi phesi lirilonse pa dziko cholembera;
Mlengalenga monse kupangidwa polembapo,
Munthu aliyense mlembi mwa ntchito,
Kuti alembe chikondi cha Mulungu mmwamba.

Momwe Mulungu wamkulu uyo Kumwamba anadzakhalira thupi ndipo anadzatenga machimo anga!

Kuti alembe chikondi cha Mulungu mmwamba
Angaumitse nyanja gwaa;
Kapena ngakhale mpukutu ukanadzazitsaponsepo,
Ngakhale utambasulidwa mlengalenga mpaka mlengalenga.

⁶⁴⁶ Ndipo kuti awapange olandira a chipulumutso ichi chiyembekezo chotsimikizika, Iye analumbira pa Iyemwini kuti Iye adzatiwutsa ife mu masiku otsiriza, nkutipatsa ife Moyo Wamuyaya. “Ndipo palibe munthu yemwe angawakhwathule iwo kuchokera mdzanja Langa.” Amen.

Tiyeni tipemphere.

⁶⁴⁷ Kodi ndinu olakwa pa kukankha chikondi Chake? Kodi inu mwaukana Umunthu Wake wodala, Mmodzi wamkulu uyu yemwe anakupangani inu chomwe inu muli? Ndipo tsopano inu muli apa, mmawa uno, mpaka apa mu moyo, ndipo izo zikukupatsani inu mwayi. Kodi inu mukufuna kuti muzikhalabe moyo? Pali njira imodzi yokha yoti mukhalire moyo, ndiyo kukhulupirira pa Ambuye Yesu. Ngati inu, kuchokera mu mtima wanu, mukukhulupirira kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu ndi

kumuvomereza Iye ngati Mpulumutsi wanu, ndi kukhulupirira kuti Mulungu anamuukitsa Iye kwa chilungamitso chanu, ngati inu mukufuna kuti muzivomereze izo pa maziko amenewo, izo ndi zanu tsopano.

⁶⁴⁸ Kodi inu mungakweze dzanja lanu? Moyo wina wosalapa, umene ungafune ku...-lapa, kulapa mmawa uno, kuti, “Ndikumbukireni ine, m’bale, mlaliki, pamene ife tikupita ku pemphero. Inenso ndalephera. Ine ndajowinapo mpingo, koma i—ine ndikudziwa i—ine sindinayambe ndakhalapo ndi chimene inu mukuchikambachi. Ine sindinayambe ndabadwapo mwa Mzimu umenewo, M’bale Branham. Ine basi—ine basi ndiribe Iwo, ndizo zonse. Ine ndikufuna kuti inu mundipempherere ine, kuti Mulungu apereke Iwo kwa ine mmawa uno.” Mulungu akudalitseni inu, bwana. Kodi pangakhale wina? Akuti, “Mulungu, ndipangeni ine chimene Inu mukufuna kuti ine ndikhale. Ine ndikufuna kuti Inu mukhale... Ine ndikufuna kuti ndikhale monga momwe Inu mukufunira kuti ine ndikhale. Ine ndakankha chikondi Chanu.” Mulungu akudalitseni inu, mwana.

⁶⁴⁹ Mphindi yokha tsopano.

Ngati kapezi wodzaza nyanja,
 Mlengalenga polembapo,
 Phesi lililonse cholemba;
 Munthu aliyense ntchito yolembe,
 Kulemba chikondi cha Mulungu mmwamba.
 Kungaiphwetse nyanja
 Mpukutu sungakwane zonse,
 Kuutambasula mlengalenga.

Chikondi cha Mulungu, cholemera
 nchangwiro!
 Chosayezeka changwiro!
 Chidzakhhalapo nthawizonse,
 Nyimbo ya oyera ndi Angelo.

⁶⁵⁰ Wokonedwa Mulungu, moona wandakatulo yemwe analemba mawu amenewo anali basi monga ena a okhulupirira Anu, akufunafuna, kuyesera kuti apeze mawu kuti achifotokoze icho. Ndipo izo zinalembedwa mu Baibulo, “Mochuluka, chifukwa mlaliki anali wanzeru, iye anafunafuna ndipo anaika mu dongosolo mawu ambiri.” O, momwe ife tikanakondera kukhala ndi lirime ndi mayankhulidwe kuti tingakhoze kufotokoza kwa anthu chomwe icho chiri kwenikweni, koma izo sizingapezeke pa milomo ya chivundi. Muyaya wonse, popanda kukaika ngati iwo ukanakhoza konse kuwulula icho, momwe Mulungu wa Kumwamba anabwerera pa dziko lapansi kuti adzapulumutse ochimwa osauka, otaika, omvetsa chisoni.

⁶⁵¹ Ine ndikukupemphani Inu, Atate, kuti kupyolera mu mawu pang’ono osasweka awa, kapena mawu oswekawa mmawa

uno, momwe ine ndikananenera, kuti winawake wapeza mtendere ndi chikhutitso ndi chitonthozo champhamvu, yemwe wathawa kufuna pobisala. Ndipo mulole moyo wawo uzikike ku lonjezo limenelo lomwe Mulungu analumbirako, kuti Iye akanadzawaukitsa iwo pa tsiku lotsiriza. Manja angapo apita mmwamba, mu nyumbayi, momwe muno mu kachisi uyu. Mulungu, apatseni iwo chiyembekezo chokhazikika icho, pakali pano. Mulole iwo azikike pa Thanthwe la mibadwo. Ziribe kanthu kuipa kwake momwe ingati izikankhira ndi momwe timabwato tawo tingati tizilumphira, iwo ali ndi nangula, lonjezo la Mulungu. Apo iwo akhala, “Mulungu ananena Izo. Iye sangakhoze kunama.”

652 “Iye amene amva Mawu Anga,” omwe ine ndayesera kuti ndiwalalikire mmawa uno, “ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, Yehova, ali nawo Moyo wosatha; ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.”

653 O Inu Wamuyayayo, adalitseni amenewo lero. Ndipo mulole munthu aliyense mkati muno yemwe sali pansi pa Magazi, moyo wawo sunatembenezidwe konse, mulole izo zichitike pakali pano, Ambuye. Inu muchite chozizwitsacho. Onsewo ndi Anu. Iwo aperekedwa kwa Inu. Ine ndikupemphera kuti Inu mupereke izo kwa iwo, Moyo Wamuyaya. Mulole, tsikulina, uko ku gombe linalo, pamene mmodzi ndi mmodzi ife tikupita kudutsa mu chigwachi, mulole ife tikakomane uko komwe iwo sadzakanena konse “ndapita” kenanso.

Tsiku lina ife tidzabwera ku mtsinje pa
kutsekera kwa nthawi,
Pamene maganizo otsiriza a chisoni ali atapita;
Padzakhala pali winawake akuyembekezera
amene adzatisonyeza ife njira,
Ine sindidasowa kuti ndidzawoloke Yordani
ndekha.
Wina, aziyembekeza andisonyeze njira,
Sindzawoloka Yordani . . .

654 Onse omwe ali nacho chiyembekezere chimenecho, kwezani mmwamba manja anu tsopano pamene inu mukuwelamutsa mitu yanu.

Ine sindi . . .

Tsopano zingomamupembedzani Iye. Uthenga watha. Kodi inu simuli okondwa? Mulungu analumbira kuti Iye sakanati . . . Mulungu analumbira kuti Iye adzakakomana nanu kumeneko.

Yesu anafera machimo anga;
Pomwe mdima ine . . .

Kodi inu mukuti chiani? Mbola yapita.

Iye andiyembekeza,
Sindzawoloka Yordani ndekha.
Nthawizina ndimasiyidwa, ndi kulema . . .

Zingomamupembedzani Iye tsopano.

Ziri ngati amzanga onse apita;

Kodi inu munayamba mwagunda pa malo amenewo?

Pali lingaliro limandisangalatsa.

Kodi lonjezolo linali chiani?

Sangalatsa,
Sindzawoloka Yordani . . .

⁶⁵⁵ Tsopano, ana a lonjezo, zingomamupembedzani Iye chifukwa chochita izo.

Sindzawoloka Yordani ndekha,
Yesu anafera machimo onse;

Chikuchitika ndi chiani tsopano?

Ndikawona mdima, Iye andiyembekeza,
Sindzawoloka Yordani ndekha.

“Pamene ine ndidzafika pa mtsinje.” Wina aliyense wa inu akubwerapo. Pali mdima waukulu, wakuda uli apo patsogolo panu. Icho ndi chitseko chachikulu. Inu mudzapita mkati mmenemo, limodzi la masiku awa, mwinamwake tsikuli lisanathe, mwinamwake mpingo usanatseke mmawa uno. Inu mukhala mukupita mkati mmenemo. Nthawi iliyonse yomwe mtima ukugunda, inu muli sitepe imodzi moyandikirapo.

Koma pamene ine ndidzawona mdima, Iye
adzakhala akundidikirira pamenepo,

Iye anati Iye akanadzatero. Iye analumbira kuti Iye adzatero.

Sindzawoloka Yordani ndekha.

⁶⁵⁶ O Ambuye Wodala, mitima yathu ili yodzaza, mmawa uno, mpaka posefukira.

⁶⁵⁷ Kuganiza za pamene kugunda kuti kusiye, ndipo anamwino nakanikizira chotsamira pa mutu wanu. Ndipo manja anu, inu osakhoza kuwasuntha aponso. Manja anu atasandulika chisanu. Ana anu, amayi anu, okonedwa anu akufuula ndi kumalira. Chitseko chachikulu icho chikukankhika motseguka, kutsidyako. Iye adzakhala akudikira.

⁶⁵⁸ Davide anati, “Ngati ine ndiyala kama wanga ku hade, Iye adzakhala ali kumeneko.” Ine sindidzasowa kuti ndidzaoloke iwo ndekha. Pamene kufaira kwa mtsinje kudzayamba kufaira mu nkhope yathu, Mulungu adzatenga bwato lamoyo, adzatilondolera ife kuti tiuwoloke iwo. Iye analonjeza kuti Iye akanadzatero. Davide mneneri anati, “Eya, ngakhale ine ndiyenda mchigwa cha mthunzi wa imfa, ine sindiwopa choipa

chirichonse. Inu muli ndi ine. Ndodo Yanu ndi chibonga Chanu, zimanditonthoza ine.”

⁶⁵⁹ Ambuye, ndife okondwa kwambiri lero, kuti ife tinaphatikizidwiramo olandira lonjezo. Lero ife tiri nawo mkati mwathu Moyo Wamuyaya, chifukwa ife tikuwakonda Ambuye Yesu ndipo tamukhulupirira Iye, ndipo tawavomereza Mawu Ake ndi kuphunzitsa Kwake. Ndipo Iye wapereka kwa ife, monga chisindikizo cha chikhulupiroo chathu, Mzimu Woyera, chisindikizo cha Mzimu Woyera. Chikhulupiroo chathu mkati mwathumu chazikika. Ndipo ngakhale nthawi zambiri ife tiziyenda mu mithunzi yamdima, nthawi zambiri ife tizipunthwa poyenda mnjira, koma nangula wathu akugwirabe. Muli chinachake mmenemo, uko kutali, chomwe chikuwoneka kuti chikutsogolerabe, chikuti, “Zisunthirani mtsogolo. Ife tikupitirirabe.”

⁶⁶⁰ Mulungu, tidalitseni ife. Ife tikukusowani Inu. Tisungeni ife nthawizonse okhulupirika ndi owona mpaka nthawi yomwe Inu muti mutidzere ife, ife tidzakutamandani Inu kudutsa mu mibadwo yosatha. Ndipo tsiku limenelo pamene ife tidzaima pa dziko lapansi...Mapazi ake odala sanayambe agunda pa dziko lapansi panobe. Apo Iye ataima pamenepo, mu mlengalenga; ndipo oyera ndi owomboledwa ochokera ku mibadwo yonse, kudutsa mu ulonda uliwonse, woyamba, wachiwiri, wachitatu, wachinai, wachisanu, wachisanu ndi chimodzi, ndi wachisanu ndi chiwiri, onse ataima pamenepo atavekedwa mu chilungamo Chake; ife tidzamuveka Iye Mfumu ya mfumu ndi Ambuye wa ambuye, ndi kumadzaimba nkhani za chiwombolo izo. Mitima yathu yosaukayi izidzanjenjemera pamene ife tizidzayang’ana pa Iye yemwe anatikonda ife ndipo anadzipereka Yekha chifukwa cha ife. Pamene ife tinali osakondeka ndi ochimwa, Khristu anafa kuti ife tikakhoze kupulumutsidwa. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izo, Atate, mu Dzina la Khristu. Amen.

⁶⁶¹ Inu mukumukonda Iye? O, momwe Iye aliri weniweni. Kodi inu simukungomverera ngati kuti inu mwanjiraina mukanangoti muike mikono yanu momukumbatira Iye? Kodi inu simukanangokonda kuti mungokwawa kupita apo ndi kukakhudza mapazi Ake, inu mukudziwa?

⁶⁶² Inu mukudziwa, pankakhala anthu ena ankabwera ku misonkhano yanga ku Phoenix, Arizona, kumati, “Ine ndikanafuna kuti ndikambirane naye Iye zithe. Ine ndikanakonda kuti ndinene, ‘Ambuye, Inu munandikonda ine pamene njira yanga inafika posawoneka chotero.’” Ine ndikanangokonda kuti ndikambirane naye Iye zithe ife tisanawolokereko. I—ine ndikufuna kuti ndimuwone Iye. I—i—ine ndikungofuna kuti ndimuwone Iye. Kuganiza za momwe ine ndikumverera, momwe mtima wanga wosaukawu

uti udzanjenjemerere pamene ine ndidzamuwona Iye ataima pamenepo.

⁶⁶³ Ine ndakhala mowirikiza ndikudabwa, “Ine ndikukhumba ndikanalimva Liwu ilo likuti, ‘Bwerani kwa Ine, nonse inu omwe muli kuvutikira ndi kulemedwa kwambiri. Ine ndikupatsani inu mpumulo.’”

⁶⁶⁴ Ine mwinamwake sindidzalimva ilo kwenikweni monga Iye anayankhulira ilo apo, koma ine ndikufuna kuti ndimumve Iye akuti, “Ili ndi tsiku lotsiriza. Izo wazichita bwino, wantchito wanga wabwino ndi wokhulupirika, tsopano lowa mu zisangalalo za Ambuye zomwe zinakonzedwera kwa iwe.” Kuyambira motalika bwanji?

⁶⁶⁵ “Kuyambira pamene inu munapulumsidwa?” Ayi m’bale.

⁶⁶⁶ “Kuyambira pa maziko a dziko, pamene Ine ndinakuwonani inu ndipo ndinakudziwiranitu inu, ndipo ndinakudzozereranitu inu ku Moyo Wamuyaya,” inu munadalitsidwa pamenepo. “Onse omwe Iye anawadziwiratu, Iye anawaitana.” Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] “Onse omwe Iye anawaitana, Iye anawalungamitsa. Iwo omwe Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa kale ulemerero.” Ndi inu pamenepo. Iye anatiidziwiratu ife, anatiitana ife, anatilungamitsa ife, ndipo ife atapatsidwa kale ulemerero limodzi ndi Iye, pa mapeto a dziko, tikupita ku mphotho yathu. Kodi sindinu okondwa? [“Ameni.”] Zedi. Izo zingakupangitseni inu kumukonda Iye. Pamene inu simukanakhoza kudzithandiza nokha, ndipo apa Iye anabwera ndipo anadzakuchitirani inu izo.

⁶⁶⁷ *Chodala Chikhale Chimango Chomwe Chimamangiriza, Mlongo Gertie.* “Mitima yathu mu chikondi cha Chikhristu,” pamene ife tiri ndi chiyanjano chaching’ono ichi cha kupembedza pano tsopano, kenako ife tikuti tiwapempherere odwala. Mulungu akudalitseni inu. Inu omwe munakwezera manja anu kwa Khristu mmawa uno, inu kapezeni malo anu oti muzikamupembedza, zikamutumikirani Iye.

⁶⁶⁸ Tsopano, tiyeni tizingomupembedza Iye tsopano, monga osonkhana, nonse inu Amethodisti, mpingo wa Mulungu, Assemblies of God, Achipresbateria, Achilutera, Achikatolika. Tonse palimodzi tsopano, tiyeni tiziyimba tsopano.

Nchodala ndi chimango
 Cha mitima mchikondi cha Chikhristu;
 Chiyanjano cha apachibale
 Chiri chonga Chakumwamba.
 Ku mpando wa Atate,
 Titsanulira pemphero lathu;
 Mantha, chiyembekezo, zolinga nzimodzi,

Chithonhozo nzosamala zathu.
 Pamene tisiyana,
 Zimatipweteka mkati;
 Koma tidzalumikizanabe . . .

Ndi angati Achimethodisti, Achibaptisti, ndi nonse?

Kuyembekeza kudzakomananso.

⁶⁶⁹ Kodi izo sizikukuchitirani inu ubwino? Tiyeni tipotoloke apo ndi kugwirana chanza wina ndi mzake tsopano, pamene ife tiri tiyiimba iyo kachiwiri.

Pamaso . . .

Gwiranani chanza, winawake kumbuyo kwanu, kutsogolo kwanu, mbali iliyonse.

. . . mpando,
 Titsanulira pemphero lathu;
 Chithonhozo nzosamala zathu.
 Pamene ife tisiyana,

Ife timakondana wina ndi mzake.

Izo zimatipatsa . . .

Ndikukhumba msonkhano ukanamangopitirira? Mukuona? Ndi momwe ife tikuganizira.

. . . ululu wa mkati;
 Koma tidzakhala olumikizanabe, mwa
 mmodzi,
 Kuyembekeza kudzakomananso.

Ngati sikunonso, pa Tsiku lalikululo ilo ife tidzakomana.

⁶⁷⁰ Tsopano, Atate, landirani kupembedza kwathu mmawa uno. Tengani Mawu ndi kuwabzala Iwo mu mitima ya okhulupirira. Mulole iwo asamangokankhidwira uku ndi uko, ndipo lero mmwamba ndi mawa pansu, koma mulole Mawu awa apeze malo awo opumira mu mtima wa wokhulupirira aliyense. Kuti azidziwa izi, kuti, “Mulungu analumbirira mwa lumbiro, ndipo pali zinthu ziwiri zosasintha. Kusasintha kwa Mulungu, ndiko kuti, ndi zosatheka kuti Iye aname, kuti olandira a chipulumutso ichi akhoze kukhala ndi chiyembekezo champhamvu ichi, chokhazikika ndi chotsimikizika, nangula mu moyo.” Podziwa ichi, kuti, “Mulungu anationjeza ife, mwa lumbiro lolumbiridwa. Chimodzi, kuti Iye sangakhoze kunama; chinacho, Iye analumbira lumbiro pamwamba pa icho, kuti Iye adzatiukitsa ife pa tsiku lotsiriza ndi kutipatsa ife Moyo Wamuyaya.” Podziwa, kuti, “Ife titaitanidwa kale, kuti Iye ananena kuti Iye anatiidziwa ife asanaikidwe maziko a dziko, ndipo anatikonzeratu ife kuti tidzakhazikitsidwe monga ana kudzera mwa Yesu Khristu. Ndipo Iye anatiidziwiratu ife. Iye anatiyitana ife. Ndipo pamene Iye anatiitana ife, Iye anatilungamitsa ife.” Ife sitingakhoze kudzilungamitsa tokha,

kotero Iye anatilungamitsa ife mwa imfa ya Mwana Wake yemwe. “Iwo omwe Iye anawalungamitsa, Iye anawapatsa kale ulemerero.” Mawu anayankhulidwa kale. Ndipo ife tiri pa ulendo wathu kokha, tikupita limodzi, tikusangalala pa njira yathu waku Ulemerero.

⁶⁷¹ Apatseni anthu chikhulupiriro, ndipo mulole zizolowezi zazing’ono ndi zinthu zomwe zatsalira pa anthu, mulole izo zisansidwe kuzichotsa pa iwo, mmawa uno, ndi Mawu awa a Mulungu omwe ali nangula wa moyo, okhazikika ndi otsimikizika. Mulole iwo adzisanse ku zizolowezi zawo, kupsya mtima kwawo kwapang’ono. Ndi zinthu zomwe zakhala... Monga Paulo ananena, mu gawo lopitirira la uthenga mu masiku pang’ono, “Tiyeni ife tiike pambali katundu aliyense, ndi tchimo lomwe limatifooketsa ife mophweka, kuti ife tikhoze kuthamanga ndi chipiriro liwiro lomwe laikidwa patsogolo pathu; tikuyang’ana kwa woyambitsa ndi wotsirizitsa wa chikhulupiriro chathu, Yesu Khristu, Yemwe anayesedwa mu machitidwe onse monga ife tiriri, komabe wopanda kuchimwa.” Iye analolezedwa kuti ayasedwe, koma Iye sanagonjere kwa yeserolo. Ndipo ife timayesedwa kuti tichimwe, koma osati kuti tigonjere konse. Chifukwa Moyo umene uli mkati mwathu ndi nangula wa kopita kwathu Kwamuyaya, ndipo ife tikuzigwira izo mopatulika kwa mtima wathu.

⁶⁷² Tsopano, pali ochuluka omwe Satana wawasautsa ndi zosautsa. Ife tikukonzekera kuti tiwapempherere iwo, Atate. Mulole iwo, pamene iwo azidutsa apa pansi pa Mawu a Mulungu lero... Mawu ofunikira aja omwe akhala akulalikidwa, Baibulo kuperekera umboni, Angelo a Mulungu ataima pafupi, ndipo Mzimu Woyera waukulu, pamwamba pa zonse, waima pano kuti uchitire umboni kwa Mawu. Tsopano, Atate, pamene iwo azidutsa pansi pa Mawu a lonjezo, mmawa uno, mulole iwo achoke pano kuti akakhale bwino. Kuti achotse zothandizira kupenya zawo, kuti ayisiye mipando yawo n—ndi machira pomwe iwo akhala akugonapo, ndi kuti angopangidwa kukhala bwino. Perekani izi, Ambuye. Mulole iwo abwerere ku msonkhano wotsatira umene iwo akulolelwa kuti akabwera, kapena ku mipingo yawo yomwe, akusangalala, kusonyezera zinthu zazikulu zomwe Khristu wachita. Izi ife tikutumikira kwa ulemerero wanu, mu Dzina la Yesu. Amen.

⁶⁷³ Ine ndi woti ndipepese chifukwa cha lonjezo lomwe ine ndinalipanga, kuti mmawa uno ife tikhala ndi mutu wa 7, koma ine sindinafike kwa iwo. Ndipo ife tiyenera kuti tipereke kanthawi pang’ono pano k—kwa izi, kwa mzere wa pemphero. Ndipo tsopano, usikuuno, Ambuye akalola, ife titenga mutu wa 7, ndi kupezamo yemwe Melkizedeki uyu anali. Ndi angati akanafuna kuti adziwe? O, ife tikungopita molunjika kumene kwa Iye, kukapeza ndendende basi yemwe Iye ali. Ndipo Lemba limanena yemwe Iye ali. Mukuona?

674 Ndipo Scofield anati uwo unali “unsembe.” Zingatheke bwanji izo kukhala unsembe, ziri zopanda chiyambi kapena mathero? Inu mukuona, iwo sunali unsembe. Uyo anali Munthu, Melkizedeki (dzina), Munthu.

675 Monga, osati kusawasamala, koma a Christian Science amati Mzimu Woyera ndi “lingaliro.” Ndipo Baibulo limati, “Iye, Mzimu Woyera.” Ndipo *Iye* ndiyo nauni yaumunthu. Ndi Munthu; osati lingaliro. Ndi Munthu. Mwamtheradi.

676 Ndipo Melkizedeki ndi Munthu, Munthu yemwe analibe chiyambi cha masiku kapena mathero a zaka. Iye analibe ngakhale bambo kapena mayi, kapena kochokera. Ndipo ife tipeza yemwe Iye ali, Ambuye akalola, usikuuno, mwa Mawu. Kodi inu mukumukonda Iye? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] O! “Mawu Anu ali nyali ya panjira yanga ndi kumapazi anga.” O!

677 Tsopano, inu mukuti, “M’bale Branham, ine sindikuzimvetsa zonse Zimenezoz.” Ngakhalenso ine.

678 Koma, nthawi ina, ine ndinali kulalikira uko mu Kentucky. Ndipo kwa ena obwera mwatsopano, ndi Achikatolika ndi ena osiyana, omwe mwina simungamvetse momwe zinthu zakuya izi, zonona za Lemba. Ine ndakhala ndikulalikira pa machiritso Auzimu. Msungwana wamng’ono wopanda-nsapato anabweretsa . . . Iye sanali wa usinkhu wa zaka fiftini, anali ndi mwana wamng’ono, ndipo iko kanali ndi khunyu. Ine ndinati, “Chavuta ndi chiani, mlongo, ndi mwana wanuyu?”

679 Anati, “Iko kali ndi zodzigwedeza.” Iye samadziwa kuti ati, khunyu. Iye samadziwa choti azitchule izo.

680 Kanthu kakang’onoko mwinamwake sikanayambe kavalapo nsapato, mu moyo wake. Wokonedwa wa mwamuna wina, tsitsi lalitali likulendewera pansu. Ine ndinati, “Kodi iwe ukukhulupirira?”

681 Ndipo maso aang’ono, otuwa mwachitsulo awo anayang’ana pa ine. Iye anati, “Eya, wawa. Ine zedi ndikukhulupirira.”

682 Ine ndinakatenga kamwana kakang’onoko. Ndipo pamene ine ndinali kukapempherera iko, iko kanasiya kudzigwedeza. Unhu. Ndipo iko kanatuluka, kanatuluka.

683 Tsiku lotsatira, ine ndinali ndikusaka agologolo, uko kumbali ya phiri. Ine ndinamumva mwamuna wina atakhala pamenepo akuyankhula, chimacheka chachikale chikukukuma. Ndipo ine ndinazembera uko. Ine ndinali ndikusaka agologolo. Iwo anali akuyankhula za ine, atakhala pamenepo, akutafuna fodya ndi kumalavula. Masamba akuwuluka, monga choncho. Ndipo iwo anali akuyankhula zokhudza, tsopano, zokhudza msonkhano usiku wapambuyo pake. Mmodzi wa iwo anati, “Ine ndamuwona mwana ameneyo. Ine ndinadzera kumeneko, mmawa uno. Iye sakudzigwedeza, panobe mmawa uno.”

Mukuona? Anati, “Izo zinali zenizeni.” Ndipo iye anali akulavula.

⁶⁸⁴ Ndipo iwo anali ndi mifuti itatsamira pa mtengo, chotero ine ndinaganiza ine kulibwino ndidzizindikiritse ndekha. Inu mukudziwa, iwo anali ndi kutsutsana pamenepo, nawonso. Kotero, ine ndinayenda kupitako. Ine ndinati, “Mmawa wabwino, abale.”

⁶⁸⁵ Munthu wamkulu kwambiri uyo, amawoneka kuti amayankhula, iye anali akutafuna fodya mkamwa mwake, monga *choncho*, ali chakumbali monga *choncho*, ndipo ali ndi khosi lalikulu, lalitali. Ndipo iye anali atavala chipewa chachikulu chachikale, anachikokera icho pa nkhope yake. Iye anayang’ana apo ndipo anandiwona ine. Iye anafikira apo ndipo anachitenga icho, anachichotsa icho, nati...[M’bale Branham akumeza—Mkonzi.] Anameza fodya wotafuna uja, anati, “Mmawa wabwino, abusa.” Mukuona? Inde, bwana. Kulemekeza. Ndipo uko nkulondola. Momwe iye aliri moyo naye, ine sindikudziwa, koma iye anatero.

⁶⁸⁶ Chotero, usiku wotsatira, ndikubwerera, uko kunali mwamuna yemwe ankafuna kuti atsutsane ndi ine pang’ono. Iye amapita ku mpingo womwe sumakhulupirira mu machiritso Auzimu. Chotero, uwu unali mpingo wa Methodist, White Hill, Kentucky. Chotero i—iye anapita k...Iye anali ataima kunja. Iye anali ndi nyali mdzanja lake. Ndipo iye anati, “Ine ndikufuna kuti ndinene chinachake, mlaliki. Ine sindingakhoze basi kuvomereza Izo, chifukwa ine sindikutha kuziwona Izo.”

⁶⁸⁷ Ine ndinati, “Inu simungathe kuziwona Izo?”

⁶⁸⁸ Iye anati, “Ayi.” Anati, “Ine ndi munthu wodwala, mwiniwanga. Koma,” anati, “ine sindikutha basi kuziwona Izo.”

Ine ndinati, “Kodi inu mumakhala kuti?”

Iye anati, “Uko ku Big Renox.”

Ine ndinati, “Chabwino, inu mukafika bwanji kwanu?”

Iye anati, “Chabwino, ine ndichita kuyenda popita kwathu.”

Ine ndinati, “Kodi inu mukukhoza kukuwona kwanuko?”

Iye anati, “Ayi, bwana.”

Ine ndinati, “Kuli mdima kwambiri usiku uno, kuli mitambo.”

Iye anati, “Inde.”

Ine ndinati, “Inu mupita chotani kwanu?”

Iye anati, “Ndi nyali iyi.”

Ine ndinati, “Nyali siikusonyeza kuwala njira yonse mpaka ku nyumbayo.” Ine ndinati, “Inu mupita chotani?”

Iye anati, “O, ine ndiziyenda ndi nyaliyi.”

689 Ine ndinati, “Ndi zimenezo. Inu muli ndi kuwala kwa nyali tsopano, ndipo nthawi iliyonse yomwe muzisunthira mbali *iyi*, kuwala kukhala kukusonyezabe patsogolo panu. Ngati inu mukhala mukupitirira kuyenda, kuwalako kukhala kukupita ndi inu.”

690 Ndipo inu muchite zimenezo mmawa uno, inu mukufuna Khristu, Wansembe Wamkulu, Wokhalira pakati wa kudwala kwanu, kapena matenda anu, kapena moyo wanu. Inu mwina simungazimvetse Izo. Ife sititero. Koma ife tinalamulidwa kuti “Tiziyenda mu Kuwala pamene Iye ali mu Kuwalako.” Inu mupange kuponda kumodzi mu Kuwalako. Ndipo pamene inu mukhala ndi Kuwala limodzi nanu, Kuwalako kuziwalira mpaka tsiku langwirolo. Iko kuzikusungirani inu njira patsogolo panu.

Ndipo ife tiziyenda kukwera mu msewu
waukulu wopambana wakalewu,
Kuwausa kulikonse komwe ndipita,
Ine ndibwino ndikhale ndi Chikristu
chachikale, Ambuye,
Kuposa chirichonse chomwe ine
ndikuchidziwa

Munayamba mwaimvapo nyimbo yakale iyo?

Palibe china chonga Chikristu chachikale,
Chikondi cha Akhristu kuti uzichiwonetsa;
Ife tikuyenda mu msewuwaukulu wopambana
wakale,
Kuwausa kulikonse komwe ife tikupita,
Ine ndibwino ndikhale Chikristu chachikale,
Ambuye,
Kuposa chirichonse chomwe ine
ndikuchidziwa,

691 Ine ndimangoikonda iyo. Chabwino. Tsopano ife tikuti tipempherere odwala. Ife sitiri. . .Ife sitimadzinenera kuti ife tingakhoze kuwachiza odwala. Ngati ife tikanamatero, ife tikanakhala tikumanena chinachake cholakwika. Munthu wodwala aliyense muno anachizidwa kale. Icho ndi chomwe Lemba linanena. “Ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Kodi uko nkulondola? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

692 Wochimwa aliyense yemwe ali muno, mwinamwake mungakhale muli wina, inu mwakhala mutapulumsidwa kuyambira pamene Yesu anafa. Koma inu musati mudzafu kuno kumene mwayi wanu unaikidwa patsogolo pa inu, kuti mupite mu Kukhalapo Kwake ndiye nkumakayesera kuzilandira Izo. Izo zinapangidwira kwatsopano. Pakali pano inu muyenera kuti muzilandire Izo. Ngati inu mutapite kudutsa Magaziwo, ndiye simuli kanthu koma. . .Inu mwaweruzidwa kale, chifukwa inu mumaweruzidwa ndi momwe inu munachitira nacho Chitetezero

cha Ambuye Yesu Khristu. Mukuona? Inu, inu mukudziweruza nokha pamenepo.

⁶⁹³ “Chotero Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Chotero, palibe kanthu komwe ine ndikanakhala nako, kuti kakuchizeni inu. Palibe kanthu komwe mpingo ukanakhala nako, kuti kakuchizeni inu. Chinthu chokha chomwe ife tikanakhoza kumachipempherera ndi ichi, kuti chikhulupiriro chanu chisalephere, kuti inu mubwere ku guwa mmawa uno kuti mumulandire Khristu ngati Mchiritsi wanu, momwe inu munachitira kuti akhale Mpulumutsi wanu. Ndipo popanda chirichonse. . . Mulungu amachita zozizwitsa. Iye amasonyeza chizindikiro chachikulu. Akhungu, ogontha, osayankhula, chirichonse, amachizidwa pomwe pano pa kachisiyu. Koma kaya izo ziripo kapena ayi, ife tikuwavomereza Iwo, mulimonse. Nthawi zambiri zinthu zimenezo zimakhala mwa masomphenya.

⁶⁹⁴ Ndi angati anali pano pafupi ma Lamlungu atatu apitawo, kapena anai, pamene bambo anabwera pano, ali limodzi wakhungu ndi wolumala, kapena atakhala mu mpando wopanda mtsempha womuimitsa. Ndipo ine ndisanachoke kunyumba, ine ndinamuwona iye mu masomphenya, “Kuti kukakhala kuli bambo kumeneko, watsitsi lakuda, likuchita imvi. Mkazi wake ndi mkazi wowoneka-mokopa, wa pafupi usinkhu wa zaka sikisite. Iye abwera ndi kukhala akulira,” ndipo iye akandifunsa ine. “Ndi kuti ndibwerere ndi kukamupempherera mwamuna wake.” Iye anakhala apo pomwe.

⁶⁹⁵ Ndipo ine ndinabwera uko. Ine ndinanena kwa ena a abale anga kuno, “Muchipenye ichi.”

⁶⁹⁶ Ndipo pamene ife tinapita mmusi ku guwa, ena anali atapemphera. Pamene ine ndinapita kuti ndikapemphere, ine ndinayenda apo pomwe ndi kubwerera mpaka kuno. Ndipo mkazi wake anauka ndipo anabwera ndendende basi momwe Ambuye ananenera kuti izo zikanadzakhala ziri. Anthu akuyang’anira, kuti awone ngati izo zikanati zichitike mwanjira imeneyo. Izo sizinayambe zalepherapo. Ndipo kotero pamene iye anayenda. . .

⁶⁹⁷ Ndinafika pozindikira, kuti bambo, Dr. Ackerman, uko ku Birdseye, Indiana, anali yemwe anamutumiza iye kuno; yemwe ali wa Chikatolika, ndipo mnyamata wake ndi wansembe mu monastere kumeneko ku Meinrad Woyera. Ndipo Dr. Ackerman ndi mzanga wosaka naye, ndipo iye anamutumiza munthuyo abwere kuno. Ndipo Ambuye anandisonyeza ine bambo wamutu wakuda yemwe akanamutumiza iye, koma ine sindinkadziwa yemwe iye anali.

⁶⁹⁸ Ine ndinati, “Kodi ameneyo anali Dr. Ackerman?”

⁶⁹⁹ Iye anati, “Iye anali.” Mukuona? Ndiyeno bamboyo. . .

⁷⁰⁰ Ine ndinati, “Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE.” Ndinapita mmusi. Ine ndinati, “Bwana, imirirani.” Ali limodzi wakhungu ndipo sankakhoza... iye... M—msempha womuimitsa unali utatha. Iye sankatha kudziyimika yekha monga choncho. Mukuona? Anali mwa njira imeneyo kwa zaka, anakhala ali kwa a Mayo ndi konse kozungulira. Ndipo ndinangopemphera pemphero pa iye, ndipo ndinamudzutsapo iye. Apo iye anapita, akuyenda kupita modutsa.

⁷⁰¹ Poyamba iye anati, “Ine sindikukhoza kukuwonani inu.” Ndiye iye anafuula, “Inde. Ine ndikukhoza.” Maso ake anadza potseguka apo. Iye anakhala ali wa chiorthodox, mkazi wake wa Chipresbateria.

⁷⁰² Anthu ena amaganiza kuti “Achipresbateria samafuula, ndi Achiorthodox.” Inu mukanati muwamve awo. Zedi. Iwo anali akufuula ndi kumakumbatirana wina ndi mzake. Anabwerera ndipo anatenga chikuku chake, ndipo anayenda akutuluka ndi kumatsika masitepe, basi monga momwe munthu wina aliyense, angakhoze kuwonera ndi kumayankhula n—ndi zina zotero.

⁷⁰³ Ndinalandira kalata yochokera kwa iye, kapena anaimba, tsiku lina. Ine ndikukhulupirira, M’bale Cox anapita kwa iye. Anati, “Maso ake anali ndi kugirigisha kotentha.” Ndithudi. Ndi msempha, misempha yopenyera ikumera ndi kubwerera ku moyo, inu mukudziwa, ndi iyo kutenga malo ake. Thembererolo linali litachotsedwapo.

⁷⁰⁴ Ngati inu mutangochilola chirengedwe kutenga njira yake, ngati patati pasakhale china chochitchinga chirengedwecho, ndiye i—icho chikhala ndi kuchita kwathunthu. Ngati inu mutakhala ndi chomanga pa nkono wanu, chikuletsa kuyenderera, dzanja lanulo potsiriza lifa. Tsopano, chifukwa, mwachirengedwe, iwo ungakhale bwino bwino ngati inu mutangowusiya iwo wokha. Koma chinachake chasokoneza chirengedwe. Ndiye, ngati inu simungachiwone icho, palibe njira yomwe adokotala angachigwirire icho. Pali zinthu ziwiri zokha zomwe iwo angagwirire nazo ntchito: zomwe iwo angathe kuziwona, zomwe iwo angathe kuzimvera. Ndi chinthu chokha chomwe iye angagwirire nacho ntchito: chomwe iye achipenya ndi chomwe iye achimvera.

⁷⁰⁵ Ngati iye sangakhoze kuchiwona icho, ndiye icho chiyenera kukhala chauzimu. Ndiye pali, chinthu chokha chomwe chingathe, chinthu chimodzi chomwe chingachitike; ife timapemphera, Khristu amalichotsa thembererolo, amamuthamangitsira Mdierekezi kutali, ndipo izo zimayamba kumakhala bwino bwino, wabwino. Kukhala bwino, ndipo ndi zonse zomwe ziri kwa izo. “Mu dzina langa iwo adzatulutsa ziwanda.” Kodi uko nkulondola? Ndi lonjezo kwa mpingo. Ndi lonjezo la mphamvu. Chiani? Ndi, ndi Kukhalapo Kwake kuli ndi ife. Tsopano, nchiani chikutiletsa ife kuti tisakhale angwiwo

mmawa uno, kuti tizichita zinthu izo basi monga Iye ankachitira izo, ndi chifukwa chakuti ife tikadali mu chophimba. Mukuona? Koma ife tiri nako kumverera kwina apo komwe kumatiuza ife, “O, inde.” Mukuona?

⁷⁰⁶ Ndipo pamene inu mulandira machiritso anu... Ziribe kanthu zomwe chophimba chinena, ndi chimene Mawu anena. Mukuona? Ndi zimenezotu. Ndi zimenezotu. Ndipo m—m—Mawu nthawizonse ndi ochuluka ulamuliro pa chirichonse. Mawu Amuyaya a Mulungu!

⁷⁰⁷ Tayang’anani pa Sarah, chiberekero chake chitafa, usinkhu wa zaka nainte, ankakhala ndi mwamuna wake kuyambira ali pafupi sikisitini kapena seventini, opanda ana; Abrahamu, zana. Mulungu anatembenuka apo ndipo anawapatsa iwo mwana. Mukuona? Chifukwa, iwo anakhulupirira. Iwo anazitcha zinthu izo zomwe panalibe, ngati kuti izo zinalipo. Lowanimo mwanjira imeneyo mmawa uno, mzanga.

⁷⁰⁸ Ndipo usikuuno, ife tikuyembekeza... Ngati inu nonse mukudzacheza nafe, ndife okondwa kukhala nanu inu pano mmawa uno. Ndipo Mulungu akhale nanu. Ndipo ngati inu muli mu mzinda kwa usikuuno, ife tikhala okondwa kukhala nanu usiku uno pa msonkhano wina wonse uwu, wa Melkizedeki. Ndiyeno ngati inu simukhalapo, ndipo muli ndi mpingo wanu wanu, inu mupite ku mpingo wanu wanuwo. N—ndiwo malo anu antchito. Ngati inu muli wa mpingo, inu mupite kumeneko. Uyu ndi kachisi wamng’ono chabe komwe ife timasonkhana muno ndi kukhala ndi chiyanjano wina ndi mzake. Tsopano, Ambuye akudalitseni inu.

⁷⁰⁹ Ndipo Mlongo Gertie azitiyimbira ife, *Sing’anga Wamkulu Tsopano Ali Pafupi*. Ndipo kodi alipo wina aliyense pano woti apemphereredwe? Kwezani dzanja lanu, awo omwe akufuna kuti abwere mu mzere wa pemphero, kuti muike chikhulupiriro chanu kwa Khristu. Chabwino. Ngati inu mungafuole motsatira ku mbali *iyi* ya mpingo, ngati inu mungathe. Ndipo ngati iwo angakokere mpandowo pansu pang’ono pokha, m’bale, ngati inu mungathe, kuti ife tipeze malo pang’ono mmenemo ndi kukhoza kuwabweretsamo anthu chodutsa. Bwerani mpaka ku mbali *iyi*.

⁷¹⁰ Ndipo ife tikuti tipemphere tsopano, pamene ife tikuimba. Ndipo ine ndikuti ndiwafunse akulu akulu pano, a chipembedzo chirichonse kapena mpingo, mosasamala chomwe iwo uli, ngati inu mukukhulupirira mu machiritso Auzimu, kodi inu mungaima apa ndi ine pa nsanja iyi, kuti tipempherere odwala? Ife tikhala okondwa kukhala nanu. Chipembedzo chirichonse, kapena osakhala chipembedzo, kapena chirichonse chomwe inu muli, ife tikhala okondwa kukhala nanu. Mungati inu mubwere tsopano, kwa pemphero, bwerani pano ndi kudzaima ndi ine.

M’bale Neville, ngati inu mungabwere ndi mafuta.



BUKHU LA AHEBRI

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org